

M'BADWO WA MPINGO WA AEFESO

Jeffersonville, Indiana, USA

DISEMBALA 5, 1960

1 Ambuye akudalitseni inu. Wina wake mkati muno amene akuyendetsa galimoto ya mtundu wa Dodge, Dodge yatsopano. Layisensi nambala yake WX - 2129, yomwe yayimikidwa ku tsidya la msewu apo, wasiya nyali zake - nyali zazikulu ndi zina zonse - zoyaka. Ndipo ngati wina aliyense akuyendetsa galimoto imeneyo, bwanji, inu mutuluke panja ndipo mukathimitse nyali zanuzo. Iyo basi iri mbali yakumanzere kwa msewu, kupitirira kumusi ku msewu wa Eighth Street. Ine ndikuganiza kuti iyo ndi nambala ya ku New Albany, WX 2129, Dodge yofiira, Dodge yatsopano. Iyo ndi pafupi '59, '60, kapena chapenapake pamenepo. Ndipo ine sindimazindikira kuti mwina panali wina wake mkati muno, kapena wina wake wangoti basi ... kuchokera kwina kwake. Chabwino. Icho chinali. Kotero icho ndi chinthu chabwino. Tsopano, ine sindinena kuti basi awo ndi azimayi amene anayiwala chimenecho, chifukwa inenso ndimachita chimenecho.

2 Chabwino, ichi ndi chabwino kwambiri kubwereranso kachiwiri mu msonkhano usiku uno, ndikukhala nayo nthawi yopambana iyi yakuyanjana pamodzi pa Mawu. Kodi inu mukusangalala nacho ichi? Uko nkulondola. Iye basi tangokhala nayo yopambana, nthawi yopambana. Ndipo tsopano, ife tikudalira kuti Mulungu atithandiza ife kumapitiriza chitsogolo. Tsopano, m'bale wanga anapita ndipo wabweretsa bolodi yakuda apa, koma ilo ndilalifupi kwambiri. Ilo basi silikumafika pamwamba mokwanira. Kotero mawa ine ndiyesetsa kuliika ilo pamwamba apa, kulikokera ilo mokweza pamwamba, ndikulipanga ilo chonchi.... Ine ndikufuna ndijambulepo zinthu zina zosiyanasiyana zomwe ine ndikufuna kuzilongosola kotero inu basi... basi kotero kuti inu munkhale otsimikiza kuti inu mukuzimvetsa izo.

3 Apo panali Usiku watha, kapena dzulo icho chinali, mtsikana wanga wam'ng'ono, Sara Icho chinakhala ngati chokongola. Mayi ndi Ine timayang'ana pa

pepala laling'ono. Iye amatenga zolemba zanga, ndipo iye analemba chirichonse basi molondola. Yesaya, ndi Mateyu, ndi zina zonse. Ndipo kumapeto kwa pepalalo, iye anali, "Ndipo imfa ... manda analibenso nkomwe chigonjetso mwa iwo, ndipo mbola yake ya imfa inali itazulidwapo." Iye ndi wa zaka pafupi - fupi zisanu ndi ziwiri.

Ndipo ndiyeno, m'malo mokhala ndi Vumbulutso, iye anati, "Buku la kusintha." Chabwino, izo zikusonyeza kuti iwo ali ndi chidwi mukuyesera kupeza china chake, mulimonse, kodi iwo siali? Ine ndikuganiza mtsikana wamng'ono wa M'bale Collins ... iye wakhala kumbuyo uko ... kodi iwo analemba kusintha? "Tsiku la kusintha," M'bale Neville akutero. Iye akugwirizana naye m'tsikanayo. Ine ndikulingalira kuti tonsefe tikuyenera kuchita chimenecho.

4 Chabwino, ife tiri nayo nthawi yopambana kwenikweni. Kalanga ine, Ambuye akutidalitsa! Ine ndinalowa muchipinda mmawa uno kukawerenga, nditangowatumiza kumene ana kusukulu, ndipo basi ndangotuluka kumene kanthawi kapitako - kungokhala ndi nthawi yodabwitsa.

Usiku watha ndinawerenga mochedweraponso. Ndipo cha m'ma 02:30 mamawa anthu ena anatsika kuchokera kumpoto. Iwo anandizutsa ine kuti ndimupempherere mtsikana wamng'ono amene anali kufa, ndipo Ine ndikutsimikiza kuti Ambuye amulola iye kuti apeze bwino. Iwo basi atsika mtunda wonse kuchokera ku Bedford, Indiana, kudzapempha pempho kuti mtsikana wam'ng'onoyo apemphereredwe pamenepo. Amuna awiri akhala ali mu msonkhano usiku watha, kuyendetsa mtunda wonse kukwera uko, kenako mtunda wonse kutsika kubwerera; kenako mtunda wonse kubwereranso kachiwiri - kapena usiku wonse mukuyendetsa. Ndipo kotero ndichabwino kwambiri kuzindikira kuti anthu akukhala ndi chidaliro cha mtundu wotero, ndikumakhulupirira Mulungu.

5 O, iri ndi tsiku lopambana limene ife tikukhalamo. Ndipo ife tikuyembekeza, pa mibadwo ya mpingo iyi, kuti basi zikhala zikuchulukira-chulukirabe. Tsopano ife tikuyesera kuti tiziyamba basi mofulumirirako pang'ono usiku uliwonse, kotero kuti tidzituluka mwamsanga. Kodi inu mukuzikonda bwino zimenezo? Ndipo izo zimalola anthu amene ali oti apita kuntchito kukafika ku nyumba, kuti akapite ku ntchito. Usiku watha

ife timatuluka mpindi 5, 10 kudutsa pa 9 koloko, kapena Ine ndinali ndiri pafupi kumaliza. Ndipo kotero ...

Ife ndiwokondwa kukhala nawo atumiki onse otiyendera ali nafe mkati muno usiku uno, ndipo M'bale Junior Jackson, M'bale Carpenter, ndi m'bale wathu kuchokera ku tchalitchi icho, ndi ena ambiri pa nsanja pano, ndi kunjja uko mu msonkhano. Imilirani kumapazi anu, M'bale ndi Mulongo Andrew, basi kanthawi kochepa. Ambuye akudalitseni inu.

6 Ndipo ine ndinawuzidwa lero kuti mnzanga wamtengo wapatali kwambiri amene anali ndi ine mu ntchito ya umishonare, M'bale ndi Mulongo Andrew wochokera mkati mweni mweni mwa China anali mu msonkhano usiku watha.

Ndi nthawi yodabwitsa chotani imene ife tinali nayo limodzi mu Jamaica, chaka chathachi. Ife tinali

ndi nthawi yopambana kwambiri. Ine ndinali uko kwawo, ndipo kalanga ine! Ine ndikudabwa ngati m'bale ndi mulongo Andrew alipo pano usiku uno mu msonkhanowu? Nyumba ino basi siyinamangidwe bwino, kotero... inde, akhala kumapeto chakumbuyo uko. Ine ndikudabwa ngati inu mungathe basi kungoyimirira pa mapazi anu motero, M'bale ndi Mulongo Andrew, basi kanthawi kochepa. Ambuye akudalitseni inu.

Ife ndi wokondwa kwambiri kukuwonani inu, M'bale ndi Mulongo Andrew. Ine ndinayitana iwo kuti abwere chaka chatha pamene ine ndinali kumeneko.

7 Tsopano, osati kuchiyankhula icho mukukhalapo kwawo Ine ndimayenera kuti ndiyankhule zochuluka, koma ine sindiyankhula izo tsopano. Koma iwo ali omwe ine ndimawatchula amishonare eni-eni. Ngati iwo angadzalowe muno mawa usiku, iwo adzatiyankhula pano, ife tisanalowe muno. Ine ndikufuna kuti inu mumve chimene ntchito ya umishonare imatanthauza kwenikweni.

Pamene iwo anabwerera kupita mkati mwenimweni, kufikira pamene iwo analibe chinachirichonse ku ... Chabwino, ine ndikuganiza kuti izo zinali zaka ndi zaka ndi zaka iwo anali kumeneko, ndipo iwo anali asanawonepo galimoto, kapena sitima, kapena china chirichonse, kwa zaka ndi zaka. Ndipo momwe Mulongo amapangira mkate wawo

kuchokera ku ..., m'mene iye ankatakasira izo, ndi Tsopano uwo ndiye umishonare weni - weni. M'bale Andrew anali ndi singano ndi ulusi, ndipo iye anali dokotala. Iye anawasoka iwo onse pamene iwo amakhala atang'ambika. Ndipo ine ndikuganiza pamene ana ankabadwa, Mulongo Andrew anali ngati mzamba ndipo M'bale Andrew ngati dokotala. Iwo basi ankangodalira pa iwo.

8 Ndipo ndiyeno, pamene amishonare ochokera ku England, amishonare a Chipentekosite aku England, ananena kuti iwo anali okalamba kwambiri kuti abwerere ku ntchito ya utumiki Ine basi ndikuuzani inu momwe iwo aliri amishonare mochuluka. Iwo sakanatha kungotenga mpando wofewa ndikukhalapo. Iwo anabwerera kupita kumeneko mwa iwo okha, kubwerera kupita ku Jamaica; ndipo ali kumeneko kuchita umishonare tsopano. M'bale Fred Sothman ndi ine, pano, tinali ndi mwayi wopita ku nyumba kwawo ndikukacheza ndi iwo. Ndipo ndi nthawi yabwino yotani imene iwo anatiwonetsa ife - mokoma monga momwe Akhristu ayenera kuchitira.

Ndipo ine ndikukuwuzani inu, ine sindikuyankhula ichi kuti Ndi kwabwino kuti ine ndipereke mphukira yaying'ono ya duwa la rose kwa iwo tsopano kusiyana ndi nkhatu ya maluwa pa mbuyo pakuti iwo apita. Ine ndikukuwuzani inu iwo ndi akhristu eni - eni. Ndipo ine ndinamuuza mkazi wanga kuti Mulongo Andrew anali m'modzi wa azimayi Achikhristu amene ndi wokometsetsa, wabwino kwambiri, amene munthu akanatha kukumana nawo iye basi ... khalidwe lake ndi lowumbidwa mwa Khristu. Ndiponso M'bale Andrew. Kotero ndine wotsimikiza ngati inu nonse munawawona iwo pamene iwo anayimirira, ine ndimafuna Mpingo uwu wonse uwangwire iwo chanza, ndipo tiwamve iwo asanachoke.

9 Tsopano mawa, Ambuye akalola, bwanji, mawa usiku ife tiyambe pa m'badwo uwu wachiwiri wa Mpingo. Usiku uno ife tikuyamba pa m'badwo woyamba wa Mpingo. Ine ndiri wotsimikizika kuti Ambuye atisungira ife m'dalitso. Ndipo kumbukirani, monga ine ndinalankhulira m'mbuyomo, nthawi zina pa zinthu izi, ife tikhoza kukhala osagwirizana pa izo, molingana ndi machitidwe azamaphunziro a za uMulungu. Ndipo mawerengedwe anga ambiri a zaka ine ndimawatenga kuchokera kwa a zambiri yakale otsimikiziridwa, amene ... kwenikweni sali otenga mbali ina iriyonse. Iwo basi anangolembe mfundo,

chirichonse chimene icho chinali, zimene mipingo inachita. Ndipo, inde, mbali ya umulungu ya kutanthauzira, ine ndimayesera kuyiyika iyo apo inemwini, mwaubwino momwe ine ndikudziwira.

Ndipo nthawi zina, ngati ine ndayankhula mwa ukaliko kapena mopupuluma, monga choncho, Ine sindimatanthauza icho mwa njira imeneyo. Aliyense akudziwa chimenecho amene amandidziwa ine - kuti ine sindimatanthauza kuchita chimenecho. Ine basi ndimangofuna Koma, pofuna kuti Mfundo ikhazikike, kuli ngati basi kukhomera nsomali pa thabwa. Ngati inu basi mungowumatika iwo apo iwo siwugwira. Inu mukuyenera kuwukhomera iwo pansu kuwuzamitsa iwo, kuwupanga iwo kuti ugwire. Ndipo icho ndichimene ine ndikuyesera kuchichita. Kotero, ichi sichikutanthauza kuti ine ndikufuna kuyesera kusagwirizana, chifukwa ine ndimalankhula kwa zipembezo zonse, ndi zina zotero. Kotero ichi sichikutanthauza ... kuti

10 Ine nthawizonse ndimati, monga kuyika chizindikiro pa ng'ombe Ine ndikukumbukira zaka zapitazo ine ndinakhala tsiku lina pamene iwo amasonkhanitsa ng'ombe malo amodzi mu nthawi yophuka udzu, kuzitengera ng'ombe kunkhalango. Ndipo ine ndinathandizira kuwongolera ng'ombe mpaka ku ... chimene iwo amachitcha kuti mpanda wosakhazikika, pamene a Bungwe la Hereford amadyetsera Muchigwa cha Mtsinje wa Troublesome. Ndipo ine ndinakhala pamenepo ndi mwendo wanga wokolekedwa pamwamba pa nyanga ya chokhalira, kuwonerera woyang'anira monga momwe iye amayang'anira ng'ombe izi akuyenda kupyola mpanda wosakhazikikawo. Tsopano inu mukuyenera kukhala ... apo ndipamene inu mukupitirira kufika ku malo a boma. Ndipo inu mukuyenera kukhala nako kuthekera kowonjezera mulingo wa udzu inu musanayike ng'ombe pa msipu. Ndipo munda uliwonse umabweretsa udzu wochuluka motero, ng'ombenso zochuluka motero. Ndiyeno iwo atha kukhala nazo izo.

11 Tsopano, iwo amapita kupyola m'menemo ndi zizindikiritso zonse zosiyanasiyana pa izo. Zina za izo zinali ndi Bar X, Bambo Grimes amene ali moyandikana nafe apa anali ndi Diamond T - cha T, pamapeto pake Diamond. Pamenepo panali Lazy K uja, kumtunda koyambira kwa Mtsinje wa Troublesome. Chathu chinali cha Turkey Track. Pansi pa ife

basi panali cha Tripod. Ndipo apo panali mitundu yonse ya zizindikiro imene imadutsa kupyola pa chipata chimenecho.

Ndipo Ine ndinazindikira kuti woyang'anira uja samapereka chidwi kwenikweni ku zizindikiro zija. Iye samaziyang'ana izo. Nthawi zina izo zimakhala mbali ya kumanzere kwa ng'ombe, kotero iye samatha kuchiwona chizindikirocho. Kotero, icho sichinali chimenecho Iye amayang'ana chizindikiro, koma chinthu chimodzi chimene iye amatsimikizika nacho chinali choti: kuti panalibe ng'ombe imene imadutsa pamenepo pokhapokha iyo ikhale ndi ndolo ya magazi mu khutu lake. Iyo imayenera kukhala yamtundu wa Hereford weniweni kapena iyo siyikanalowa mu nkhalangomo. Chizindikiro chija sichimapereka kusiyana kwenikweni, koma inali ndolo ya magazi ija.

Ndipo ine ndikuganiza kuti ndi m'mene ziti zidzakhali pa chiweruzo. Sichidzakhala kuti ndichizindikiro chanji chimene ife tavalala, koma Iye azidzafuna ndolo ya magazi. "Pamene Ine ndiwona magazi, Ine ndidzapyola pa inu."

[M'bale Branham akuyankhula kwa M'bale Gene zokhudza maikolofoni -] Tsopano, kodi ine basi ndalakwitsa pang'ono, Gene, Kodi ine ndatero? Kubwezanso. Chabwino ... uko nkusinthanitsa pakati pa ziwirizo, kodi uko nkulondola? Chabwino. Zikomo inu m'bale Gene, chabwino.

12 Tsopano, ife tiyesera kuti tituluke mofulumiranso kachiwiri usiku uno, kotero kuti ife tidzabwereranso mawa usiku, ndikudzatenga mibadwo iyi. Ndipo Ine ndikukuwuzani inu, ndizolimba kwambiri kwa ine kuzisunga zinthu zazikulu izi zimene zagona mphepete mwa msewu - basi kuyesera kuzitulutsa izo zonse mu usiku umodzi. Inu mukudziwa, uwo ndi mtundu wa chikhalidwe changa., koma ife basi tikuyenera kuzisunga izo m'mbuyo pang'ono, mpakana usiku uliwonse.

Tsopano, ife tisanayambe kutsegula Bukhu Lalikululo, ndidabwa ngati ife tikanayimirira kwa kanthawi kochepa, posintha malo, monga ife tikuyimirira, awo amene angathe. Ndipo tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano, mwaulemu, kwa liwu la pemphero.

13 Atate wathu wakumwamba, ife kuyandikiranso kachiwiri Mpando Wanu Waukulu Wachifumu Woyera, kubwera popanda kugwedezeka kwa chikhulupiriro chifukwa Ife tikubwera chifukwa tinayitanidwa kuti tibwere. Ife sitinganene kuti ife tikubwera mu dzina la Mpingo wina wake, kapena chipembedzo; kapena mu dzina la mpingo uwu, kapena mu dzina la ife eni, chifukwa ife sitingakhale otsimikizika ku chimenecho - kaya ife tipeza kumvana uku ndi Mulungu kapena ayi. Koma pamene Yesu anatiwuza ife, "Inu pemphani Atate chirichonse mu dzina langa, Ine ndidzachita icho," ndIyeno ife tikudziwa kuti tikubwera mu Dzina la Yesu. Inu mutimva ife, Atate.

Ife ndiwokondwa kwambiri monga ife tikuwerenga za iwo amene anafera uthenga mumasiku amene anapita, m'mene iwo anatsindikizira umboni wawo ndi magazi a iwo eni. Ndiyeno, Atate, ichi chikutipangitsa ife kumverera kuti ife tikuchita mochepa kwambiri mu tsiku ili. Ndipo ine ndikupemphera kwa Inu, Ambuye, kuti Inu mudzatikhululukira kulekerera kwathu, monga ife tiri mu ntchito yanu. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mutidzozze ife mwatsopano, monga ife tikuwerenga mu Mawu Anu, ndikuwona kuvutika kumene kunabweretsedwa mu masiku amene anapita, kupanga gulu lovomerezeka lalikulu, la Mpingo wowomboledwa la Mulungu wamoyo.

14 Ine ndikukupemphani inu, Atate akumwamba, kuti muyankhule usiku uno kupyolera mwa ife, chifukwa ife sitikudziwa choti tiyankhule. Ife basi tikudikirira, ndipo ife tikupempha pemphero iri pano chifukwa ife tiri pamaso pa Mulungu mu Mpingo Wake. Ndipo ife tikupempha kuti Mzimu Woyera umene uli pa anthu awa udzalumikiza mphamvu zake pamodzi usiku uno, ndikugwedezeka Uthenga kulowa mu mtima uliwonse. Izo zidzatipatsa ife mayimidwe a tsopano, ndi chiyembekezo chatsopano, ku m'badwo umene ukubwera. Chiperekeni icho, Ambuye, pakuti ife tikuwona mtengo wa mkuyu ukuphukira masamba ake, ndipo Israeli akukhala fuko, ndipo masiku a amitundu akutha, ndi kutsala ochepa.

Ndipo ife tikuyang'ana kukubwera kwa Muwombolo wamkulu, Ambuye wathu, Yesu Khristu. Muyende pakati pathu, Ambuye, monga momwe zinanenedwa usiku uno, Inu mumayenda pakati pa zoyika nyali. Ndiyeno muyende pakati pathu usiku uno, Ambuye, ndipo muchenjeze mitima yathu ku choyipa chimene chiri patsogolo pathu,

ndipo mutipatse ife kumvetsa kwa Mawu Anu, pakuti ife tikuzipempha izi mu Dzina la Yesu. Amen. Inu mukhoza kukhala pansu.

15 Tsopano monga ine ndakhala ndikuyankhula, tsiku lililonse ine ndimayesera kulemba zochuluka pa pepala monga momwe ine ndingathere za nthawi, malo, ndi zina zotero, chifukwa ndi chochitika chambiri yakale chimene ife tikuchiyandikira. Iyo yakhala iri mbiri. Ndipo tsopano ife tikubweranso kuyiphatikizira

iyo ku nthawi.

Tsopano, Lamulungu m'mawa ndi Lamulungu masana, kapena Lamulungu madzulo kani, ife tinali ndi nthawi ya Ulemerero. Ine ndikutsimikiza ife tinali nayo. Ine ndinali nayo ndekha.

16 Ndipo za chivumbulutso ... Tsopano kodi ife tikuphunzira chiyani? Vumbulutso la Yesu Khristu. Ndipo kodi ife tinapeza chiyani? Kuti Mulungu anawonetsa vumbulutso ndi chimene Iye anali. Chinthu choyamba chimene ife tikuchipeza mwa mavumbulutso onse, kuti Mulungu anazipanga kudziwika chimene Iye anali - kuti Yesu sanali munthu wachitatu wa utatu woyera; Iye anali utatu muchizalo. Iye anali zonse Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Ndipo ilo linali vumbulutso. Chayankhulidwa kanayi mu mutu omwewu, kuti Iye anali Mulungu wa mphamvuzonse, chimene Iye anali, amene ali, ndi amene alinkudza, mudzu ndi mbadwa ya Davide.

17 Tsopano ife tikupeza kuti, mu zinthu izi ife tikhala tikuyesera kukonza chinthu chonsecho, chifukwa ine sindikudziwa kuti ndi liti limene ife tidzamvenso izi kachiwiri - mwina osamvanso - mpakana sipadzakhalanso nthawi, ndi kudzalowerera mu umuyaya.

Ndipo tsopano, monga ine ndanena, mwina patha kukhala abale ambiri, aphunzitsi, amene adzakhala oyenerezeka kwambiri kukayankhula ichi kuposa ine, ndipo kapena kudzapeza tanthauzo lomveka bwino ku icho. Koma Mulungu wachikhazika icho pa mtima panga kuti ine ndichichite icho, ndipo choncho, ine ndidzakhala wonyenga ngati ine sindikanayankhula ndendende chimene ine ndimaganza kuti chinali cholondola, mwaona.

Kotero, ine ndimafuna nthawi zonse ndikhale wopanda vuto pamaso pa Mulungu kuti ine sindinasiye, monga Paulo ananena, kukuchenjezani inu usana ndi usiku, ndi misonzi, kuti mwina Mpingo ungakhale woyima. Ndiyeno, ngati pangakhale wina wotayika, magari ake asakhale m'manja mwanga, chifukwa ndikufuna kudzakhala opanda magari a anthu onse pa tsiku limeneli. Kotero, ngati inu musiyana, bwanji, izo basi zangokhala mu njira ya bwino ya ubwenzi, izo zidzakhala zabwino - basi. Tsopano ... koma mwina Ambuye adzaulula china chake chimene chidzathandiza tonsefe limodzi.

18 Tsopano, chinthu choyamba, ife tikuwona kuti Iye anadziwulula Yekha. Tsopano ife tikutha kumvetsetsa kuti kodi Iye anali Ndani.

Tsopano m'musimu monga ine ndinapereka lemba lokhudza kukonkha ndi ubatizo mu Dzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera kukhala ubatizo wa chiKatolika ndipo osati wa a Chiprotestant kapena ubatizo wa Chipangano cha Tsopano, ine ndi kuyembekezera kuti ndinachifotokoza icho momveka bwino. Ndipo ine ndakhala ndikufunsa ngati pali munthu wina yemwe angandisonyeze Ine gawo la Malemba pamene wina aliyense anabatizidwapo mu Baibulo - kapena mpakana Council ya Laodikaya, pamene iwo anayambitsa Mpingo wa Katolika - pamene wina aliyense anabatizidwa mu Dzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera, chonde bwerani mudiwonetse ine; ndipo ine ndidzayika pa msana panga cholembedwa kuti "Mneneri wa Wonyenga," ndipo ndidzayenda kupyola mu msewu. Tsopano ine basi sikuti ndikufuna kuzipanga izo kukhala zokhwima, koma basi kungokuwonetsani inu kuti ichi ndi chowonadi, mwaona.

19 Tsopano. Ndiyeno Baibulo likumuwulula Iye apa, kuti Iye ndi Mulungu wamphamvuzonse, Thupi pakati pathu, mwaona. Popanda Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Iyo similungu itatu, kapena Mulungu m'modzi kugawidwa malo atatu. Iye ndi Mulungu m'modzi amene amagwira ntchito mu maofesi atatu: Utate, Umwana, ndi Mzimu Woyera; Mulungu kudzichepetsa Yekha kuchokera m'munda wa Edeni, kuyesera kuzibwezera yekha m'mbuyo mkati mwa moyo wa munthu kuti akhale moyo, ndikuwapanganso iwo ana amuna ndi akazi a Mulungu kachiwiri pa modzi ndi Iye. Mulungu pamwamba pa ife, Mulungu ndi ife, Mulungu mwa ife. Uko ndiye kusiyana, mwaona.

Ndipo tsopano zinthu izo Ndipo Baibulo likuwulula chimenecho, ndipo ilo linanena za icho momveka bwino mu mutu woyamba wa Chivumbulutso, lomwe ndi bukhu lokhalo mu Baibulo (mu Chipangano Chatsopano, Chipangano chonse Chatsopano), ndi buku lokhalo limene Yesu anayikapo chisindikizo cha Iyemwini pa ilo. Ndipo Iye anati, choyamba cha icho, "Wodala ndi Iye amene awerenga, ndi Iye amene akumva." Ndipo kumapeto kwake. Iye anati, "Ngati munthu wina aliyense akachotsera gawo la iwo, kapena kuwonjezera chinachake kwa iwo, yemweyo gawo lake lidzachotseredwa mu Buku la Moyo." Kotero ndi themberero kwa wina aliyense kuchotsera chinachirichonse.

Iri ndi vumbulutso lathunthu la Yesu Khristu. Kotero, ngati ife tingamupange Iye atatu, inu mukudziwa chomwe chidzachitike, mwaona. Dzina lanu limachotsedwapo.

20 Ndipo palibe m'modzi, palibe wa Chiprotestant, palibe mpingo woyamba, umene unayamba wakhulupirirapo mwa milungu itatu. Iyo inali nkhani yayikulu ku Nicene Council, ndipo onse a iwo anayima kakasi uko, monga mwakunena. Autatu, anthu amene amakhulupirira utatu, chimene pamapeto pake chinapangidwa mu mpingo wa Katolika, iwo anapita ku utatu kwathunthu - kumupanga Mulungu kukhala anthu atatu. Ndipo apo panali iwo amene amakhulupirira kuti Mulungu anali m'modzi, ndipo anapita mbali inayo kukakhala a umodzi. Onse a iwo ndi wolakwa.

Mulungu ... Yesu sakanakhala atate ake a Iye yekha; ndipo kapena Yesu kukhala nawo atate ake, ndipo Iye ndikukhala milungu itatu. Izo sizikanagwira, chifukwa ngati Iye ali nawo atate, ndipo atatewo ndi munthu wina wapadera pambali pa Iye, ndiyeno Iye anali ... ndipo Mzimu Woyera ndi Wina Wake, Iye ndi mwana wapathengo.

Baibulo limanena kuti Mzimu Woyera ndi amene anali Atate Wake. Ndipo ngati ife tili naye Mzimu Woyera, ndiyeno Iye si Mzimu Woyera ayi - Iye ndi Atate mwa ife mu dzina la Mzimu Woyera, kugwiritsa ntchito udindowo mwa ife. Chifukwa Iwo unali mwamunthu nthawi ina, ukutchedwa "Mzimu", ukubweranso, ndipo iwo uli mwa ife tsopano. Mulungu Yehova Yemweyo, mwaona.

21 Palibenso milungu itatu.

Milungu itatu ndi chikunja, ndi chikunja chenicheni, ndipo icho chinabweretsedwa Ndipo ngati inu mungakhalepo kupyola sabata yonse, ndipo osagamula mwachangu, koma penyani, chitengeni icho ... mbiri. Mutenge mbiri zofanana ndi zimene ine ndimatenga kapena mbiri yakale ina iriyonse. Basi mulole ... tiyidziwe iyo. Mbiri zakale zonse zimagwirizana chimodzi. Awo a zambiri yakale alibe chochita ndi mbali ina iriyonse. Iwo basi amangokhala ndi chidwi mukunena mfundo, zimene zinachitika.

Ndipo penyani ndendende m'mene chinthu chimene chija chinakwawira mkati kudzera mwa Luther, ndikutuluka kudzera mwa Wesley; ndipo ndiyeno ndikuwonekera poyera mu masiku otsiriza - ubatizo wa mu Dzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Basi penyani kumene icho chikubwera kulowa mu mpingo wa Katolika; mu Mibadwo ya Mdimba kutuluka kudzera kwa Luther, kutsika kudzera mwa Wesley. Koma pakati pa Wesley ndi a Chilaodikaya kumapeto, icho chimayenera kuyikidwa poyera. Uko nkulondola.

Tsopano ... ndipo izi zonse ndi mbiri zakale, ndipo osati mbiri yokha koma ilo ndi Baibulo.

22 Ndipo tsopano usiku uno, ife tikuyandikira mibadwo isanu ndi iwiri ya Mpingo, imene inali mipingo isanu ndi iwiri mu Asia Minor pa nthawi imene buku limalembedwa. Mipingo imeneyi pa nthawi imeneyo ikuyenera kuti inali ndi zikhalidwe za mibadwo ya mpingo imene imadza, chifukwa kuti panali mipingo yochuluka kuposa imeneyo - mpingo wa ku Akolose ndi ina yambiri - pa nthawi imeneyo. Koma Mulungu anatenga Mipingo imeneyi chifukwa cha zikhalidwe zawo.

Tsopano, ife tikupeza kuti, Iye amene akuyimirira pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri za golide, Iye anali nazo m'manja mwake nyenyezi zisanu ndi ziwiri. Ndipo nyenyezi zisanu ndi ziwiri izo Iye ananena mu ndime ya 20 ya mutu woyamba kuti iwo ndi angelo asanu ndi awiri kwa mipingo isanu ndi iwiri.

23 Tsopano, mu Baibulo iwo samamvetsetsa vumbulutso ili, chifukwa ndi ubwino wanji umene ilo likanachita kwa iwo poyang'ana ndi kudikirira, ngati iwo akanadziwa kuti panadza zikwi - zikwi Yesu asanabwere? Icho sichinaperekedwe kwa iwo.

Ndipo ine ndikuyankhula kuichi, kwa inu anthu apa, inu anthu a ChiKatolika, kwa inu a Lutheran, kwa inu a Methodist, ndi ena otero, icho sichinaperekedwe kwa Martin Luther kuwala kumene kuli pa Mawu lero. Sikunaperekedwensu kwa John Wesley. John Wesley analikira kuyeretsedwa kumene Luther anakulumpha. Ndipo, kuwala kumabwera monga ife tikufunira kuwalako. Mulungu akunena izo, ndipo sizinatsegulidwire kwa ife chifukwa izo zabisidwa kwa ife kufikira tsiku lomwe Mulungu adzakhale ndikuthekera kuulula icho.

Ndikudabwa kuti kudzakhala chiyani ife titachoka. Ine ndakopeka kuti kuli zochuluka, zochuluka kwambiri kuposera zimene ife tikudziwa. Uko ndi kulondola. Pali zisindikizo zisanu ndi ziwiri, ngati ife basi titi titenge Bukhu lonse lathunthu la Chivumbulutso, zimene zasindikizidwa kumbuyo kwa Bukhu. Izo zizinalembedwa ngakhale mkati mwa bukhu. Ndipo zisindikizo'zo zikuyenera kuti zitsegulidwe mu m'badwo uno wa mpingo, ndipo zinsinsi zisanu ndi ziwiri zotsiriza zizindikirika. O, Ine ndikufuna basi ndizisunge izo zonse nyengo yozizira, ndikudutsa mu izo. Inde, bwana. Mibadwo ya mpingo isanu ndi iwiri...

24 Monga Daniele anamva mabingu asanu ndi awiri aja, ndipo ... naletsedwa ... ndipo Yohane anamva maliwu, ndipo buku ili linasindikizidwa. Ndipo kumbuyo kwa buku kunasindikizidwa ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri. Koma mu masiku oti zisindikizo izi zitsegulidwe, chinsinsi cha Mulungu chidzatsirizidwa. Mu mawu ena, Mulungu azadziwika ku Mpingo wake osati mwa anthu atatu, koma ngati munthu m'modzi. Chinsinsi cha Mulungu chidzawululidwa. Ndipo pamene icho chidzawululidwa kwathunthu, ndiyeno zinsinsi zisanu ndi ziwiri zidzawululidwa ku Mpingo; chifukwa umo mpingowo udzakhala uli pansu pa kuzodza kwa mzimu oyera - Iye akulowa ndi kutuluka, ndikumawonetsera zizindikiro zake zakuti ndi moyo ndipo ali pakati pathu, kukhala pakati pathu. Ndipo ife ndiyeno tikupembedza Khristu Wamoyo amene ali pakati pathu.

25 Osayang'ana konse Mipingo yayikulu ndi zinthu zazikulu. Pamene ife tidzafika ku m'badwo wa Pentekosite uwu, inu mudzawona ndithu pamene iwo anachiphonya icho.

Mpingo womwewo wa "Loadikaya" umatanthauza kulemera, wosasowa kanthu; ndi wamaliseche, watsoka, wakhungu, womvetsa chisoni, ndipo osazindikira icho, mwaona. Iwo ndi wotayika kutali ...

monga ndalama zazikulu, ndi nyumba, ndi zinazonse; pamene mpingo wakhala nthawizonse wakhala chonyozeka cha dziko ku dziko la pansi, wodedwa ndi anthu onse, wotayiridwa kunja, m'makwalala, palibenso pamene iwo angakhale.

Werengani; Aheberi 11, ndipo mutenge ndime zisanu ndi imodzi kapena zisanu ndi zitanu zotsiriza za iwo, - m'mene iwo anayendera muzipululu, ndikuvala zikopa za nkhoa ndi zikopa za mbuzi, ndipo anali osowa pokhala, ndiotunduzidwa, ndi kuzunzidwa, anthu amenewo uko.

Kodi umboni wathu udzayima bwanji kutsutsana ndi wawo mu tsiku la chiweruzo, mwaona, anthu amenewo mu tsiku ilo?

26 Tsopano, mu m'badwo wa Mpingo uwu, ife tiri ndi Mipingo isanu ndi iwiri. Tsopano ine ndikufuna iyo ilembedwe. Ine sindikuganiza ngati inu mungathe kuyiwona iyo kuchokera apa. Mwina, ngati ena a inu mungathe Ine ndikukayikira icho kwambiri. Koma Ine ndiyesera kuchichita icho (Ine ndikudziwa inu simukanatha, kukhala pansi mkati muno), kuchichita icho "Mibadwo Isanu ndi Iwiri ya Mpingo." Ndipo ine ndichigwirizira icho pa dzanja langa, kotero kuti inu mumvetsetse.

Icho chikuyamba ... Mpingo unayamba pa Pentekosite. Kodi wina aliyense angachikane chimenecho? Ayi, bwana. Mpingo unayamba pa Pentekosite ndi mdalitso wa Chipentekosite; ndipo iwo unadzozedwa ndi Yesu Khristu kuti upitirire mpakana tsiku lomaliza, ndi Uthenga womwewo ndi mdalitso womwewo ukugwira ntchito mwa iwo. Kutuma kwake kotsiriza ku Mpingo wake, Marko 16: "Pitani ku dziko lonse lapansi, kalalikireni Uthenga zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akakhulupirire" Kuti? Ku dziko lonse lapansi. Kwa ndani? Ku zolengedwa zonse, okuda, abulauni, achikasu, oyera, cholengedwa china chirichonse chimene icho chinali. "Kalalikireni Uthenga ku cholenedwa chirichonse. Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akakhulupirire"

Tsopano, usiku uno ife tikuyandikira ku icho basi kuyamba kuchidula icho usiku uno. Usiku uliwonse kudulako gawo lalikulu la icho, mpakana ife tidzafika ku m'badwo wa Mpingo wathu wathu.

Tsopano, ife tikupeza kuti uko kunali kutuma kwake.

27 Tsopano m'badwo wa Mpingo woyamba unali Mpingo wa Aefeso. M'badwo wa Mpingo wachiwiri unali wa Smurna. M'badwo wa Mpingo wa chitatu unali wa Pergamo. M'badwo wa Mpingo wa chinayi unali wa Tiyatira. M'badwo wa Mpingo wachisanu unali wa Sarde. Ndipo m'badwo wa chisanu ndi chimodzi unali wa Filadelfeya. Ndipo m'badwo wachisanu ndi chiwiri unali wa Loadikaya.

Tsopano, m'badwo wa Mpingo woyamba unayamba mu A.D. 53, pamene Paulo anakhazikitsa Mpingo mu Aefeso. Mu ulendo wake wa umishonare, iye anakhazikitsa mpingo kwa Aefeso, mpingo wa ku Aefeso; ndipo anali m'busa wa iwo mpakana pamene iye anadulidwa mutu mu 66, kumupanga iye kukhala m'busa wa Mpingo wa ku Aefeso kwa zaka makumi awiri kudza ziwiri. Pambuyo pa imfa yake, ndiyeno ife tikuwuzidwa kuti Paulo Woyera ... kapena, Yohane Woyera wa Umulungu anakhala m'busa wa Mpingowo, ndipo iye anaunyamula iwo kufikira mu m'badwo uno. Ndipo m'badwo wa Mpingo umenewo unafika mu 170.

28 Ndiyeno, m'badwo wa Mpingo wa Aefeso utatha, kuchokera mu A.D. 53 mpakana A.D. 170, kenako m'badwo wa Mpingo wa Smurna unayamba, umene unatha kuchokera mu A.D.170 mpakana A.D.312. kenako unabwera m'badwo wa Mpingo wa Pergamo, ndipo m'badwo wa Mpingo wa Pergamo unayamba pa 312, ndipo unatha mpakana A.D.606. kenako unabwera m'badwo wa Mpingo wa Tiyatira, ndipo m'badwo wa Tiyatira unayamba pa 606, ndipo unayenda kufika pa 1520, m'badwo wa M'dima.

Ndipo kenako m'badwo wa Mpingo wa Sarde unayamba pa 1520, ndipo unatha mpakana 1750, m'badwo wa Luther. Ndiyeno kuchokera 1750, m'badwo wotsatira umene unabwera unali wa Filadelfiya, m'badwo wa Wesley. Umenewo unayamba pa 1750 ndipo unatha mpakana 1906. Ndipo pa 1906, m'badwo wa Mpingo wa Loadikaya unalowa, ndipo ine sindikudziwa pomwe uti udzathere. Koma ine ndikuneneratu kuti iwo udzakhala

utatha pofika 1977. Ine ndikuneneratu; osati Mulungu anandiwuza ine. Koma Ine ndikuneneratu icho malingana ndi masomphenya amene ine ndinawawona zaka zingapo zapitazo, kuti zinthu zisanu za zinthu zimenezo (mwa zisanu ndi ziwiri) zachitika kale, zokudza....

29 Ndiangati amene akukumbukira masomphenya amene aja, mu tchalitchi muno? Ndithudi. Amene amanena m'mene Kennedy adzasankhidwire mu zisanu zotsiriza izi; m'mene azimayi adzavomerezedwere kuponya voti; m'mene Roosevelt adzalitengere dziko lapansi ku nkondo; m'mene Mussolin adzapitire ku Ethiopia, kuwukira kwake koyamba ndi m'mene adzalitengere ilo. Icho chidzakhala chimaliziro. Iye adzafa zitatha izo. M'mene malingaliro aakulu akayendetsedwe ka zinthu adzaukire, ndipo zonse ndikubwerera ndi kudzalowa mu Chikominisiti - za chi Hitler, ndi Mussolini, ndi za chi Nazi, ndi ena otero, onse adzabwerera ndikudzalowa mu Chikominisiti.

Ndipo pasanathe zaka khumi ndi chimodzi, masomphenyawo anati ife tidzapita ku nkondo ndi

Germany, ndipo Germany adzazunguliridwa ndi mpanda wa konkire - Mzere wa Maginot. Icho chinachitika basi njira yomweyo. Anati, kenako zitatha izo zidzachitika kuti sayansi idzawonjezereka kwa kukulu, mpakana kuti iwo adzapanga galimoto Magalimoto adzakhala mowoneka kwambiri ngati dzira nthawizonse. Ndipo masomphenya amenewo ananenedwa pompano pamene Mpingo wa Khristu ukuyimapo tsopano pa nyumba yakale ya ana amasiye. Charlie Kern, mwina alipo mu nyumba ino usiku uno, amakahala pa malopo panthawiyo.

Lamulungu lina mamawa, pafupifupi leveni koloko, icho chinachitika. Ndipo masomphenyawo anati izo zidzachitika kuti iwo adzapanga galimoto imene siidasowa kukhala ndi chiwongolero mkati mwake. Iyo izidzawongoleredwa ndi mphamvu ya mtundu wina. Iwo ali nayo iyo tsopano. Iwo ali nayo iyo tsopano - mphamvu ya maginito, kulamulira ndi makina a m'mphepo. Iwo sakuchita ngakhale Basi kungowalamulira makina anu za komwe inu mukupita. Iyo ikutengani inu inunokha. Inu simukusowa kuyiwongolera iyo.

30 Tsopano. Ndipo iwo anati mkati umo panthawi imeneyo padzakhala mkazi wamkulu amene adzayime mu United States. Ndipo iye anavala, ndi wokongola, koma Iye anali wankhanza mu mtima mwake. Ndipo Ine ndiri nawo apadera, pamasomphenya, ngakhale pepala ya chikasu, inati, "mwina Mpingo wa Katolika." Ndipo kuvomerezedwa kwa azimayi kuponya voti kudzathandizira kusankha munthu wolakwika ku fuko lino - ndipo icho ndichimene iwo achita. Ndendende. Tsopano, iwo anati ichi chidzakhala chiyambi. Tsopano chinthu china chimene iwo ananena, kuti mwamsangamsanga zitatha izo ine ndinawona fuko lino likukhala ngati likuyaka, basi kungophulitsidwa mutidzidutswa.

Tsopano, ngati zinthu zina zonse zinachitika, kotero chinthu chinachinso chidzachitika. Ife tiri pa Ndi chifukwa chake ine ndiri pano usiku uno, kuyesera kuchibweretsa ichi, ndi kuchikhazika icho kwa anthu awa ku Jeffersonville, chifukwa ine ndi kukonzekera kulowa mu ntchito ya umishonare kachiwiri posachedwapa, ndipo sindikudziwa ndi nthawi yanji imene ine ndingayitanidwe ndikuchotsedwapo, kapena kukwatulidwa. Ife sitikudziwa chimenecho. Ndipo Ine ndikufuna ndikhale wotsimikizika kuti Ine ndausiya Mpingo ukudziwa ora lomwe iwo akukhalamo, chifukwa Mulungu wamphamvuzonse adzandifunsa ine za icho.

31 Tsopano Mpingo uliwonse mwa Mipingo iyi, Malingana ndi Lemba apo, unali ndi M'ngelo ndipo M'ngeloyo anali a Ndi angati amene akudziwa chimene M'ngelo amatanthauza? Iye ndi Wamthenga. Wamthenga. Ndipo apo panali Angelo asanu ndi awiri ku Mipingo isanu ndi iwiri - kutanthauza Amithenga asanu ndi awiri. Tsopano, ndipo panali nyenyezi mu dzanja lake. Ndipo mu dzanja lake khumi ndi ziwiri izi ... nyenyezi zisanu ndi ziwiri izi, uko kunali kuwonetsera kuwala kwa kukhalapo kwake mu tsiku la usiku limene ife timakhalamo; monga nyenyezi zimanyezimiritsa dzuwa ku dziko lapansi, kulipangitsa ilo kuwala kotero kuti ife tingayende, ndikumayenda mu nthawi ya usiku.

Tsopano ife tapeza kuti mkati mwa nthawi iyi kuti wina aliyense wa Angelo awo anali ndi udindo komanso malo. Ndipo, abale, usikuuno ife sitikufika ku chimenecho, chifukwa Ife tikumudziwa Mngelo uyu wa Mpingowu woyamba; koma chidzakhala

chinthu cha chinsinsi ndi cha ulemero kuchipeza, ndikuchichotsa kuchitulutsa mu mbiri ya kale pamaso panu, Angelo a Mipingo ina.

M'ngelo wa Mpingo woyamba anali Paulo Woyera. Iye anawuyambitsa iwo, Wamthenga wa Mulungu. M'ngelo wa Mpingo wa Aefeso anali Paulo Woyera. Mpingo

Tsopano chifukwa chimene ine

32 Tsopano, enawa, inu mukhoza kusavomereza. Koma ine ndinakhala kumeneko kwa masiku ndi masiku, pansu pakudzoza, mpakana ine ndinamverera kukhudza kwa Mzimu Woyera ndikundidzoza ine ku icho. Icho ndi chifukwa chake ine ndikudziwa. Ndipo penyani amuna awa amene anatengedwa, ngati inu muli wazambiri yakale. Amuna omwewo amene ine ndiri nawo pano, ndikuzindikira mwa vumbulutso kuti iwo anali Angelo ku Mpingo, anali ndi utumiki wofanana umene awa anauchita pachiyambi. Ndipo utumiki umenewo sungasithe. Iwo ukuyenera kukhala Pentekosite nthawizonse.

33 Tsopano, a zambiri yakale amene akhala muno sagwirizana nane pazamunthu uyu. Koma pa Mpingo wa Smurna, Ireniasi ndi amene ine ndikumudziwa kuti ndi amene anali M'ngelo wa tsiku limenelo. Polycarp - ambiri a inu mudzanena kuti anali Polycarp, mwina. Inu munena kuti anali iye. Koma Polycarp anatsamira kwambiri ku bungwe, ndi Chikatolika kunena za chipembezo.

Koma Ireniasi anali munthu amene amayankhula mu malirime, ndipo anali ndi mphamvu ya Mulungu, ndipo zizindikiro zinali kumutsata iye. Iye anali Mngelo wakuwala wa Mulungu. Ndipo iye anakukokabe kuwalako pambuyo pa kupachikidwa kwa Polycarp, kapena kuphedwa, kapena kuphedwa mwa chiwembu. Kenako ... Ireniasi anali m'modzi wa wophunzira wake, ndipo Polycarp anali wophunzira kwa Paulo Woyera ... kapena, Yohane Woyera. Ndipo kenako, Ireniasi anatenga malo ake, ndipo iye anabweretsa kuwala.

34 Ndipo m'ngelo wakuwala waku Pergamo anali Martin Woyera wamkulu. Ine sindikukhulupirira kuti

panali munthu wa mkulu amene anayamba wakhalapo pa dziko lapansi, kunja kwa Yesu Khristu koposera Martin Woyera. Mphamvu? Achiwembu

anabwera kwa iye kuti adzadule mutu wake. Iye amakhulupirira mu zizindikiro ndi zozizwa, ndi mdalitso wa Pentekosite. Ndipo pamene iwo anapita ... kuti akamuphe iye, Iye anavula chophimba chake naperekera khosi lake kwa iwo. Ndipo pamene wachiwembu anasolola lupanga lake kuti adule mutu wake, mphamvu ya Mulungu inamumenya ndi kumukankha iye kumugwetsera uko kutali ndi iye, ndipo wachiwembuyo anakwawa pa mawondo ake ndikupempha chikhululukiro. Amen. Iye anali M'ngelo kwa Mpingo.

Zinthu zina, penyani m'mene iye m'modzi mwa abale ake anali atapachikidwa. Iye anali ali pa msewu kuyesera kuti amupeze iye, kuti awone chimene chinachitika. Ndipo pamene iye anafika kumeneko, iwo anali atamupachika kale. Iye anali akuzendewera ali wakufa, ndipo maso ake anali atatong'okera kunja kwa mutu wake. Iye anapita kwa wakufayo, ndipo iye anagwada pa maondo ake, ndipo iye analambatitsa thupi lake pa mwamba pa wophedwayo kwa ora limodzi, kupemphera kwa Mulungu. Ndipo mphamvu ya Mulungu inabwera kwa munthuyo. Ndipo iye anadzuka, namugwira dzanja lake, ndipo anayenda onse awiri monga chonchi.

Iyo ndi mbiri ya kale, basi ngati ya George Washington, Abraham Lincoln, kapena zina zonse. Iyi ndi mbiri ya kale. Inde, bwana. Martin Woyera anali M'ngelo wa Mpingo wa Pergamo umene ... ukwati wa Mpingo. Umene ukuwatenga iwo kuwalowetsa mu Chikatolika pambuyo pa izo.

35 Mngelo wa Mpingo wa Tiyatira anali Columba. Mngelo wa Mpingo wa Sarde, Mpingo wakufa Mawu oti "Sarde" amatanthauza Wakufa - Kutuluka ndi dzina limene si dzina Lake, koma dzina loti iwe uli ndi moyo; koma iwe ndiwakufa. Penyani m'mene iwo anaubweretsera ubatizowo mu tsiku ilo, mwaona; kuchokera ku chimenecho. Mngelo wa Mpingo wa Sarde anali Martin Luther, wokonzanso woyamba.

Mngelo wa Mpingo wa Filadefiya anali John Wesley, wamthenga. Ndipo Mngelo wa Mpingo wa Loadikaya sakudziwika panopa. Adzaziwika tsiku lina, koma mwina iye a ... [Gawo lopanda kanthu pa tepi.] iye amene ali nalo khutu ... [gawo lopanda kanthu pa

tepi.] Zindikirani uwu ndi m'badwo umene ife tikukhalamo. Mulungu adzachita maweruzo azimenezo.

36 Tsopano. Zindikirani, tsopano, ndipo ife tsopano tidzafika ku Malemba, kubwerera m'mbuyo ku m'badwo wa Mpingo Woyamba. Tsopano, ine ndikufuna ... Ine ndiri ndi zinthu zocheza zimene ndalemba apa zimene Ine ndikukhumba inu mukanazimvetsera mwatcheru.

Mpingo Woyamba, Mpingo wa Aefeso, ntchito za mpingowo, zimene Mulungu anawatsutsa nazo iwo, zinali ntchito zopanda chikondi. Mphoto yawo inali mtengo wa moyo. Mpingo wa Smurna unali Mpingo wozunzidwa unadutsa mu mazunzo. Mphoto inali korona wa moyo. Mpingo wa chitatu, Pergamo: m'badwo wa chiphunzitsa chabodza, bodza la Satana, maziko a ulamuliro wa chipapa, ukwati ku Mpingo ndi dziko. Mphoto inali mana obisika ndi mwala woyera. Mpingo wa Tiyatira unali Mpingo wa kudolola kwa upapa, Mibadwo ya m'dima. Mphoto inali mphamvu ndi ulamuliro wa mafuko, ndi nyenyezi ya m'mawa. Ako kanali kagulu kaocheza kamene kanadutsa umo.

37 Mpingo wa Sarde unali m'badwo wa kukonzanso, wa misionare wamkulu ... kapena osakhala wa misionare, koma maina obisika. Iwo anali ndi maina awo awo. Ndipo mphoto inali chovala choyera, ndi dzina pa Bukhu la Moyo limene liti lidzabwere mu chiweruzo. Ife tinalankhula zimenezo tsiku lina, Buku la Moyo. Inu mukuyenera kuweruzidwa kuchokera mu Buku la Moyo. Oyera amatsandulizidwa, ndikutengedwa popanda ilo. Iwo samapita ku ilo.

M'badwo wa Mpingo wa Filadefiya unali m'badwo wa chikondi cha pa abale, m'badwo wa kutuma kwakukulu, ndi m'badwo wa umisionare waukulu - khomo lotseguka. Ndipo mphoto inali mzati, kuwulula maina a Mulungu, anali mu ... mkati mwa m'badwo umenewu, pamene iwo unatha m'ma 1906. Chabwino.

M'badwo wa Loadikaya unali Mpingo wofunda, wolempera, wokhala nawo katundu wochuluka, wasasowa kanthu, koma unali watsoka, wosauka, wakhungu, ndi wovutika ndi wamaliseche. Ndipo mphoto inali kukhala pa mpando wachifumu ndi Ambuye, onse amene agonjetsa m'badwo umenewo.

38 Tsopano kuti tiziswe izi usiku uno, kuti tikuwonetseni inu pang'ono zokhudza utimiki madzulo ano, ife titenga mutu wachiwiri, m'badwo woyamba. Tsopano Iye waululidwa, ndipo ife tikudziwa kuti Iye ndi ndani. Iye ndi Mulungu.

Tsopano, m'badwo wampingo unayamba, monga ine ndinanena, cham'ma 53 mpaka 170, ndipo (a) mzinda wa Aefeso, umodzi mwa mizinda ikuluikulu yaku Asia, nthawi zonse wotchedwa mzinda wachitatu wa chikhulupiriro cha ChiKristu. Woyamba unali Yerusalemu; wachiwiri Antiyokeyo; ndi wachitatu, Aefeso. (c) Mzinda waukulu wa zamalonda ndi mabizinesi. (e) Boma linali la chiRoma. (f) Chilankhulo chinali chi Herene.

A zambiri yakale amakhulupirira kuti Yohane, Maria, Petulo, Andreyana, ndi Filipo onse anakwiridwa kumeneko. Ndipo Efeso anali wodziwika chifukwa cha kukongola kwake.

39 Chikhristu ku Efeso panali pamene Ayuda anakhazikika ku Efeso, ndipo icho chinayambitsidwa pakati pa A.D. 53 kapena 55. Chikhristu chinadzalidwa kumeneko ndi Paulo Woyera. Pambuyo pake Paulo Woyera anatha zaka zitatu ku Efeso. Chiphunzitsa cha Paulo chinabereka kukopa kwakukulu kwa okhulupirira ku Efeso.

Wotsatira, Timoteo anali bishop woyamba wa Mpingo wa ku Efeso. Paulo anawulemba kalata Mpingo wa ku Aefeso. Munthawi ya Paulo iwo unali Mpingo waukulu. Efeso amatanthauza ... dzina lomwelomwelo la Efeso limatanthauza "Kulekerera. Kutayirira. Kubwerera m'mbuyo." Oyitanidwa ndi Mulungu, "Mpingo wobwerera m'mbuyo." Kubwerera ku utumiki usiku uno, ife titenga mutu wa 2, m'badwo wa Mpingo woyambirira. Tsopano Iye waululidwa, ndipo ife tikudziwa kuti Iye ndi ndani. Iye ndi Mulungu.

Mulungu anazindikira koyamba ntchito zawo, ndi chilemetso chawo, ndi chipiriro chawo. Mulungu anadzudzula umoyo wawo, kuleka chikondi chawo cha poyamba, pobwerera mbuyo, posakhalanako kuwala.

Efeso siunali Mpingo wonyengedwa. Iwo unagwa wokha posapitiriza kukhala mu chikondi changwiro.

40 Chidule cha zipatso za Efeso: wopanda chikondi, kutsogoleredwa ku chitsokeretso. Malonjezo: paradizo amene analonjezedwa kwa ogonjetsa, a oyera mtima a ku Efeso mu m'badwo wa Mpingo, operekedwa ku Mtengo wa Moyo.

Pano pali chinthu chokongola. Mtengo wa moyo ukutchulidwa katatu mu Genesesi, katatu mu Chivumbulutso. Nthawi yoyamba pamene iwo unatchulidwa mu Genesesi munali mu Edene, ndipo Khristu anali Mtengowo. Maulendo atatu amene iwo unatchulidwa mu Chivumbulutso, anali Khristu mu paradizo. O, izo nzolemera. Ambuye adalitse.

41 Tsopano ife tidzayamba mutu wa 1 wa Efeso ... kapena, ndime yoyamba ya mutu wa chiwiri, Mpingo wa Aefeso:

Kwa Mngelo wa Mpingo wa ku Efeso Lemba; zinthu izi zimene azinena Iye Amene agwira nyenyezi zisanu ndi ziwiri mu dzanja Lake lamanja, amene amayenda pakati pa zoyika nyali zisanu ndi ziwiri za golide;

Yohane ndiye amene anali wa mthenga pa nthawi imeneyo. Amene amayenda pakati pa zoyika nyali zisanu ndi ziwiri za golide anali Yesu Khristu, Mulungu Wamphamvuzonse. Kodi Iye akuchita chiyani? Iye sananene kuti Iye amayenda muchoyika nyali chimodzi. Iye amayenda pakati pazonsezo, kodi zimenezo zimatanthauza chiyani? Kutu Iye ndi Mulungu yemweyo, dzulo, lero, ndikunthawi zonse, ndi mu m'badwo wa Mpingo uli wonse kwa wokhulupirira wina aliyense. Iye akubwera ndi Mzimu Woyera ku m'badwo wina uliwonse ndi ndi kwamunthu aliyense - yemweyo dzulo, lero, ndi kunthawizonse.

42 Kugwira mu dzanja Lake la manja, - "dzanja la manja" kutanthauza ulamuliro Wake ndi mphamvu - kugwira mu dzanja lake la manja [kukhala pansa, kulamuliridwa] amithenga asanu ndi awiri ku mibadwo ya Mpingo isanu ndi iwiri. O, Ine ndikuchikonda chimenecho. Kumuwona Iye akuyenda mozungulira kudzera mu mibadwo ya Mpingo iyi, Khristuyo, kudzipanga yekha kudziwika kwa anthu ake kutsika kudzera mu Mibadwo ya Mdimba, kutsika kudzera mu m'badwo wina uliwonse; pamene Mpingo unayamba kukhala mwa mwambo ndikutulukamo, ndi ena kupita njira ina enanso ina. Koma kagulu ako

kakang'ono ka mpingo kanagwiritsitsabe, ndipo Khristu amagwira nawo ntchito kutsimikizira Mawu Ake; mpaka kufika ku mapeto.

43 Ichi ndi chopheka kwambiri kuwona kuti kodi chimene ife tiri nacho lero tachipeza bwanji, pamene inu muyamba kuwerenga ichi.

Tsopano pachiyambi (ndikukhulupirira onse ... ngati inu mungawone pamwamba apa), apa pali m'badwo wa Mpingo umodzi. Umenewo ndi wa Pentekosite. M'badwo wa Mpingo wachiwiri, wachitatu, wachinayi, wachisanu, wachisanu ndi chimodzi, m'badwo wa chisanu ndi chiwiri wampingo. Tsopano ngati inu mungachizindikire ichi choyandikira kwambiri, Mpingo unayamba pa Pentekosite. Ndiangati amene akukhulupirira chimenecho? Kodi inu mukuwona chimene chinachitika pa Pentekosite? Ndiyeno ife tiyang'ane Mpingo monga m'mene iwo ukupitirirabe kuyenda chotsika iwo basi ukuyamba kuzilala mochulukirapo, mopitirirapo, mopitirira, pang'ono, motsika ngati chonchi, pamene Mpingo weniweni ukutuluka.

Tsopano, Khristuyo ... ziribe kanthu kaya Mpingo ndi waung'ono chotani, "Paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana pamodzi mu Dzina langa, Ine ndidzakhala pakati pawo." Pamene iwo asonkhana pamodzi mu chiyani? Kodi ndi mu dzina la Methodist? Mu dzina la Baptist? Mu dzina la Achipentekosite? Mu Dzina la Yesu. Paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana pamodzi, ziribe kanthu kaya

ndiwochepa motani. Ndipo iwo azidzakhala ochepa kwambiri mu masiku otsiriza mpakana pamene Iye anati Iye akuyenera kuti adze mwamsanga ndikudzayifupikitsa ntchitoyo, kapena kuti sipadzakhala thupi limene lidzapulumutsidwe ku Mkwatulo. "Paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana mu Dzina Langa"

44 Tsopano, ulendo woyamba, atumwi. Tsopano, ife tikuwona kuti ichi ndi chiyambi, Pentekosite. Iye akuyenda mozungulira. Mulungu wamkulu yemweyo, zizindikiro zazikulu zomwezo zimayenera kuchitika zonse kutsika kudzera mu mibadwo iyi yonse chifukwa Iye amayenda pakati pa m'badwo wina uliwonse. Kudalitsa chiyani? Anthu ake amene asonkhana mu dzina lake. Ine ndikufuna inu muone mu ichi, monga ife tikudutsa kudzera

mu Mpingo. Mpingo uwu unali nalo dzina la Yesu. Mpingo uwu unali nalo Dzina la Yesu. Mpingo uwu unali nalo Dzina la Yesu, ndipo Mpingo uwu unalitaya ilo.

Mpingo uwu unatuluka, mu m'badwo wa Luther, "ndi dzina loti inu muli ndi moyo koma inu muli akufa," ndikumapitabe kutsika pansu mpakana kumapeto kwa m'badwo uno. Ndipo pakati pa m'badwo uwu ndi m'badwo uwu pak hazikitsidwa khomo lotseguka, limene likubweretsanso dzina ilo kawiri ku Mpingo. Tsopano penyani, ndipo muwone ngati icho sichiri choonadi, pamene ife tikulowa umu mu Malemba ... Ma ... pakati pa mibadwo....

45 Tsopano mawa usiku ine ndidzayesera kuchikhazika ichi pamwamba apa kotero kuti ife tonse tizidzatha kuchiwona icho, ndipo ine ndidzabwera mwina mawa madzulo ndikudzajambula zina mwa madongosolo zimene ine ndikufuna kuti ndiyankhule kwa inu. Ndipo ngati aliyense wa inu ali nazo mbiri zakale, zibweretseninsu izo, kapena mutenge zolemba zanu ndipo mupite mutsikire ku nyumba yowerengeramo mabuku, kapena kwinkwaka, ndipo mutenge mbiri ndikuyiwerenga iyo, ndipo muwone ngati izi ziri zolondola.

46 Tsopano ndime yoyamba, kodi Iye akuchita chiyani? Iye akuwalonjera iwo.

Kwa M'ngelo wa Mpingo wa ku Efeso [kwa Yohane] Lemba; zinthu izi anena Iye amene wagwira nyenyezi zisanu ndi ziwiri mu dzanja Lake la manja, Amene akuyenda pakati pa zoyika nyali zisanu ndi ziwiri zagolide;

Awa ndi malonje. Tsopano, ndime yachiwiri ndi ndime yachitatu, Iye akuyamikira iwo:

Ine ndikudziwa ntchito zako, ndi chilemetso chako, ndi chipiriro chako, ... ndi kuti sukhoza kulola oipa; ndipo unayesa iwo amene azitcha okha atumwi, osakhala atumwi, ndipo waapeza iwo onama:

Mwaona, chitsokeretso icho chinali chitayamba kale kulowamo, mu m'badwo woyamba uwu. Chinali chitayamba kale, komweko, chifukwa Mpingo wosankhidwa ndi

woona umene umafuna kusunga malamulo a mu Baibulo, ndi kusunga Mawu amene Yesu ananena mu umboni wake ... iwo anali atayamba kale kutulukamo.

China chake chinayamba kuchitika, ndipo panali aphunzitsi onyenga amene anauka - anthu amene amaphunzitsa zolakwika, zosemphana ndi Malemba, kuyesera kubweretsamo china chake kapena kuwonjezera china chake. Icho ndi chifukwa chake chimene Iye anaperekera vumbulutso iri ku Mpingo, ndipo anati, "Aliyense amene achotsera kapena kuwonjezera kwa iwo, gawo lake lidzachotseredwa mu Buku la Moyo." Uko ndi kutayika, m'bale.

Basi osasewera ndi Mawu a Mulungu. Basi ... ziribe kanthu kaya Iwo amuvulaza ndani, kapena Iwo avulaza chiyani. Basi kungowayankhula iwo mulimonsemo, basi mu njira yomwe iwo alemberedwa apo. Iyo ndiye njira Ife sitikusowa chachikulu china chake. Ife sitikufuna wansembe aliyense kapena chinachake kuti chiwamasulire iwo kwa ife. Mulungu, Mzimu Woyera, ndi amene ali wotanthauzira. Iye amapereka kutanthauzira.

47 Tsopano, ngati inu mukuzindikira, kutembenuka kuchokera ku zoipa ndikupeza Aneneri onyenga, pambuyo pa izo iwo anatsimikiziridwa onyenga, kukhala nawo maonekedwe aumungu Onani m'mene Mpingo unayamba kukhala wa mwambo pa nthawi imeneyo? Iwo anayamba kukhala ngati kuphwasuka. Anthu amene anali pansu pa kudzoza kwa Mzimu Woyera anayamba kuwapangitsa anthu kukhala ngati akuwaseka iwo.

Chabwino, kodi Yesu sananene, "Odala muli inu pamene iwo akukuzuzani inu chifukwa cha chirungamo"? Iye sananene kuti ayambe kuchita mwambo. Iye anati, "Sangalalani, ndipo Kondwani mochulukana, pakuti iwo anawazunza Aneneri amene analipo inu musanabwere." Iye anachinena icho mu chiphunzitsa cha pa Phiri, mu Mateyu 5, "Odala muli inu"

Bwanji, kuwapanga anthu kuti adzikusekani inu chifukwa inu mukumukonda Ambuye Yesu, ndi mdalitso basi kuti iwo akunena zimenezo. Iwo ndi okhawa ... pamene iwo akukutembererani inu, iwo akubweretsa madalitso a Mulungu kuwatsitsa pa inu. Icho

chinmabwerera kwa iwo, monga momwe zinachitikira kwa Balamu nthawi ija. Icho chikubwereranso pa iwo.

Pamene iwo ayesera kukupangani inu choseketsa pokhala Mkhristu, bwanji, icho chimabwerera kwa iwo, ndipo Mulungu amapereka mdalitso chifukwa, "Odala muli inu pamene anthu adzakuzunzani inu chifukwa cha dzina langa." Chifukwa cha dzina lake, odala muli inu.

48 Tsopano ife tikupeza kuti iwo amafuna kuyamba ndi kulowa mu mawonekedwe a umulungu.

Tsopano, Ine nditha kuyima pano ndikunena china chake. Khulupirirani Ine ndidzatero. Kodi inu munachizindikira chitsitsimutso chirichonse Tsopano, abale otumikira, inu mufufuze ichi. Chitsitsimutso chiri chonse chimabereka mapasa, monga Yakobo ndi Rebeka anabereka mapasa Esau ndi Yakobo. Ine ndikutanthauza Isaki m'malo mwa ... Isaki ndi Rebeka, m'malo mwa Yakobo. Isaki ndi Rebeka anabereka mapasa. Atate anali woyera, amai anali woyera. Koma iwo anali ndi anyamata awiri amene anabadwa - Esau ndi Yakobo.

Tsopano, onse awiri anali a chipembedzo. Koma Esau, pamene zifika pa ntchito ndi zochita monga wa chilamulo wabwino, iye mwina anali m'nyamata wabwinoko, pa china chiri chonse, kusiyana ndi chimene Yakobo anali. Kodi inu mumachidziwa chimenecho? Yakobo basi anali m'nyamata wam'ng'ono amene amakhala pafupi ndi a mai ake nthawi zonse. Koma Esau amatuluka kunja kukagwira ntchito, amatuluka kunja ndikukapeza nyama yoti apereke kwa abambo ake akhungu okalamba amene anali Mneneri. Iye ankayesera kumusamalira iye.

Koma Yakobo anali ndi chinthu chimodzi chokha m'malingaliro ake. Iye ankafuna ukuluwo. Iye samasamala kuti kaya zikhala motalika chotani akudikirira, kapena kuti Iye amayenera kuchita chiyani. Chinthu chofunikira chimene chinali mumoyo wake unali ukulu. Ndipo Esau anaunyoza iwo.

49 Tsopano inu simukumuwona munthu wa thupi? Munthu wa thupi pamene chitsitsimutso chibwera Pamakhala anthu magulu awiri amene amaturuka mu chitsitsimutso chirichonse. Pamakhala munthu wa thupi amene amapita, ndipo iye amabwera pa guwa ndikunena kuti, "Inde, bwana, ine ndikumulandira Khristu ngati Mpulumutsi wanga." Iye amapita, ndipo iye amachita chiyani?

Chinthu choyamba inu mukudziwa, iye amakathera mu mpingo wina wabwino wozizira wamwambo, chifukwa iye akuganiza, "Chabwino, ngati ine ndijowina Mpingo, Ine basi ndikhala wabwino ngati munthu winayo. Kodi ine sindiri basi wabwino ngati wakuti - ndi wakuti? Kodi ndikusiyana kotani kumene izo zimapanga pokhapokha ngati ine ndiri mumpingo ndi kupanga chivomerezo changa?"

Bwanji, apo pali kusiyana kwakukulu. Inu mukuyenera kubadwanso mwatsopano. Inu mukuyenera mukhale nawo ukulu. Ndipo Yakobo sanasamale kuti iye adzasekedwa motani. Iye amafuna ukulu umenewo, ndipo iye samasamala m'mene iye akanati awupezere iwo.

50 Tsopano, anthu ambiri sakufuna kuwupenza ukulu chifukwa iwo akuganiza kuti iwo basi ndi pang'ono wosatchukitsa. Iwo sakufuna kuti abwere pa guwa ndikulira pang'ono, kapena kupita popanda zakudya zochepa ndi china chake chimnzake. Iwo sakufuna kuchichita chimenecho. Azimayi ochuluka ... ambiriwo, inu mukudziwa, ataphoda, iwo akuganiza kuti ngati atati alire akhoza kuzitsuka izo kuzichotsa, iwo ndikukaziyaniso izo kawiri. Bwanji, ndi ... ine sindikutanthauza kuchitchula icho mosinjirira ndipo ine ndi ndikuyembekezera kuti icho sichikumveka mwa njira imeneyo. Koma ichi ndi choonadi. Iwo basi samachifuna icho.

Iwo samafuna kubadwa mwatsopano, chifukwa kubadwa kwatsopano ndi nyansi. Kuli ngati kubadwa kwina kulikonse. Kubadwa kwina kulikonse ndi nyasi. Ine sindikusamala kaya iko kuli pati. Ngati iko kuli mukhola la nkhumba, kapena mu balani yotchisira fodya, kapena kuti kuli muchipinda chapinki chokongoletsedwa cha kuchipatala, iko ndi nyansi.

Ndipo kotero kubadwa mwatsopano ndi nyansi. Ameni. Iko kudzakupangani inu kuchita zinthu zimene inu simumaziganizira kuti inu mukanachita izo - kuyima pa ngodya ndikumamenya chisakasa, kapena kuyimba, "Ulemerero ukhale kwa Mulungu, Aleluya! Mulungu atamandike! Ulemerero kwa Mulungu!" Bwanji, inu muchita ngati wamisala. Ndichimene iko kunachita kwa atumwi. Ndichimene iko kunachita kwa namwali Maria. Iye anachita ngati waledzera. Iye anali nyansi m'mudzi. Koma zimatengera nyansi kuti moyo utulukemo. Ameni.

51 Pokhapokha ngati china chake chifa ndi kuwola, moyo sungatuluke kuchokera mu chimenecho. Pokhapokha ngati munthu afa ndi kuwola mu maganizo a Iyemwini, Khristu sangalowe mu mtima mwake. Pamene inu muyesera kuganiza za inumwini, "Tsopano, ngati ine ndingayende kupita ku gome ndikunena kuti, 'Inde, Ambuye, ine ndine munthu wabwino, ine ndidzakutengani inu. Ine ndizipereka zakhumi zanga, ine ndizichita ichi'", inu mukuyenera kuti mufe ndi kuwola pomwepo ku malingaliro anu. Mulole Mzimu Woyera alamulire ndipo basi muchite chirichonse chimene Iye akufuna kuchita ndi inu. Kuchita mwa nyasi ndi icho. Icho chikumveka moopseza - osati mosinjirira - koma ndi choonadi. Ndi njira yokhayo imene ine ndikudziwa yomwe ine ndingachikhomerere chinthucho kukupangitsani inu kuchimvetisa icho.

Kodi izo zinali nyansi motani mosiyana ndi gulu la a Yuda olemekeseka aja tsiku lija, kusiyana ndi kuwona anthu awa akutuluka kuchokera uko ndi milomo yachibwibwi? Kodi inu mukudziwa kuti chibwibwi ndi chiyani? [M'bale Branham anawonetsera chimene chibwibwi chiri.] Malilime ena, ndikuchita monga anthu oledzera, icho ndi ndendende chimene iwo amachita. Iwo amawoneka mwa nyansi. Ndipo iye anati, "Kodi amuna awa onse aledzera ndi vinyo watsopano?"

52 Koma pamene m'modzi wa iwo anazindikira, iye anati, "Lolani kuti ichi chidziwike kwa inu ndipo imvani mawu anga: Anthu awa sanaledzele monga inu mukuganizira kuti icho chiri." Koma iye analunjika ku lemba, "Ichi ndi chija chomwe chinanenedwa ndi Mneneri Yoweli: Ndipo chidzachitika mu masiku otsiriza, atero Mulungu, "Ine ndidzathira Mzimu wanga pa matupi onse,"" Iyo ndi njira yomwe Mpingo unabadwira koyamba.

Ndi angati amene akukhulupirira kuti Mulungu ndi wopada malire? Ndiyeno Iye sangasithe. Ngati ilo linali lingaliro lake la Mpingo pachiyambi, uwo ndi mtundu wa Mpingo umene Iye ati adzakhale nawo kumapeto. Iye sangasithe.

Kotero inu mungaloweze m'malo bwanji ndi kugwira dzanja, kapena kukonkha, kapena chinthu chinachake, chimene sichinachitike kumeneko? M'modzi ali yense wa atumwi anabwerera ku chimenecho. Pambuyo pa iwo kuchita

53 Mzimu Woyera unagwa pa iwo. Petulo anati, "Kodi ife tingawaletse madzi, powona kuti awa alandira Mzimu woyera monga ife tinachita pachiyambi?" Ndipo iye anawalamulira iwo kuti abatizidwe mu Dzina la Ambuye Yesu. Uko nkulondola.

Paulo anapita pamenepo ndipo anawapeza anthu akufuula, ali nayo nthawi yopambana, gulu la aChibaptisti akulemekeza Mulungu, ndipo iye anati (Machitidwe Atumwi 19), iye anati, "Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni?"

Iwo anati, "Ife sitikudziwa kaya ngati pali Mzimu Woyera uliwonse."

Anati, "Kodi inu munabatizidwa bwanji?"

Iwo anati, "Ife tinabatizidwa ndi munthu yemweyo amene anamubatiza Yesu, Yohane M'batizi."

Iye anati, "Inde. Izo sizinagwirensa ntchito." (Petulo anazisindikiza izo pa tsiku la Pentekosite. Iye anali ndi mafungulo, mwaona.) Anati, "Icho sichidzagwiranso ntchito. Inu mukuyenera kuti mubatizidwenso kachiwiri." Kutero iye anawabatizanso iwo kachiwiri, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu; nayika manja ake pa iwo, ndipo iwo anali ndi zotsatira zofanana ndi zimene iwo anali nazo pachiyambi. Mzimu Woyera unagwa, pa iwo. Iwo anayamba kuyankhula m'malirime ndi kunenera.

54 Tsopano, uwo wakhala uli Mpingo kutsika kudzera mu m'badwo.

Tsopano, izo zinayambira apa pachiyambi. "Ine ndidziwa kudekha kwako, chipiro chako choopsya. Ine ndikudziwa chimenecho. Tsopano kumbukirani, Ine ndi Iye amene amayenda pakati pa zoyikapo nyali. Ine ndikudziwa chipiro chako ndi ntchito zako, ndi

kulemedwa kwako, ndi chikondi chako, ndi zina zotero. Ine ndikudziwa zonse zimene iwe wazichita. Ndipo Ine ndikudziwa kuti iwe wawayesa anthu awa amene amazitcha okha Aneneri, Atumwi, ndipo apezeka kuti iwo ndi abodza.

"O, icho ndi chindunji, sichoncho icho? Ine sindikhala woyankha ku izo; Iye ali. Iye anati iwo anali abodza.

55 Koma baibulo linati, "Tamuyesani munthu. Ngati pali wina pakati panu amene ali wauzimu kapena m'neneri, kapena akunena kuti iye ali, Ine, Ambuye ndizadziziwitsa Ine mwini kwa iyeyo. Ine ndidzalankhula kwa iye m'masomphenya, ndi m'maloto. Ndipo ngati chomwe iye anena chichitika, ndiyeno inu mumvere iye. Inu musamuope iye, mwaona, chifukwa kuti Ine ndiri ndi iye. Koma ngati izo sizichitika, ndiyeno musamumvere iye. Iye alibe Mawu Anga," mwaona. Ngati iwo akanakhala Mawu Ake, izo zikanachitika.

Tsopano, iwo anapeza kuti anthu awa samachita monga mwa Baibulo. Mwaona, iwo amayesera kuti apeze china chake. Ine ndikufuna inu kuti muvale chisoti chanu choganizira tsopano, pamene ife tikufika ku timfundo tofunukira basi mu mphindi zochepe. Tsopano, Iye anati, "Ine ndikuona chomwe inu muli ... kuti inu muli nacho chipiro, ndi kudekha, ndi iwo. Inu mwawayesa iwo, ndipo mwawapeza iwo kuti siali Atumwi. Iwo siali."

56 Tsopano, monga Ine ndinanena poyamba, ife tisanayambe pa ichi kachiwiri, chitsitsimutso chirichonse chimabereka mapasa. M'modzi amakhala munthu wauzimu; winayo amakhala munthu wathupi wa pa dziko. "Ine ndinajowina Mpingo. Ine basi ndine wabwinoko monga wina aliyense." Ndipo chimenecho ndichimene chitsitsimutso ichi chinabereka. Chimenecho ndi chimene chitsitsimutso chiri

chonse Ndichimene cha Luther chinabereka. Ndichimene cha Ireniyasi chinabereka. Ndichimene cha Martin Woyera chinabereka. Ndichimene cha Columba chinabereka. Ndichimene cha Wesley chinabereka. Ndipo ndichimene chi Pentekosite chinabereka. Basi ndendende.

Inu mukuwona m'mene iwo apitira ku kumbewu? - kumanga matchalitchi awo ndikumapitirirabe kuchokapo, malo abwino akulu? Ndipo, zodabwitsa, kuyimirira ndikumabwerezwa nthano za Atumwi! "Ine ndikuhulupirira mu Mpingo woyera wa Roma

Katolika, ndi M'gonero wa oyera mtima." Aliyense amene akhulupirira chiyanjano cha oyera mtima ndi wazamizimu. Chiri chonse chimene chiyanjana ndi akufa ndi cha mdierekezi. Uko ndi ndendende kulondola.

Ife tiri ndi nkhalapakati m'modzi pakati pa Mulungu ndi munthu. Ameneyo ndi munthu Yesu Khristu. Uko nkulondola. Chimenecho ndi chimene Petro anayankhula.

57 Ndipo inu okondeka anthu a Katolika mumamutcha iye papa woyamba. Ndipo Petro, pokhala papa woyamba, amene anayenda ndi Yesu, ndipo ndiyeno iye anati, "Palibe nkhalapakati wina pakati pa Mulungu ndi munthu." Ndipo awa ... inu muli ndi ena zikwi khumi lero.

Ndichifukwa chiyani icho chasinthwa kwambiri choncho, ngati Mpingo uli wotsimikizika ndi wosasintha? Ndipo misa zanu zonse zimayankhulidwa mu chi Latini kotero icho sichingasinthwa? Chinachitika ndi chiyani? Ndipati mu Baibulo pamene inu mungapeze chikhulupiriro cha aPostoli? Ngati Atumwi anali ndi chikhulupiriro chirichonse chinali, "Lapani, ndipo batizidwani aliyense wainu mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhulukiro cha machimo anu." Palibenso chikhulupiriro china chimene ine ndinamvapo kuti iwo akuchidziwa, kapena kulakatula china chake.

58 Koma pamene icho chibwera ku Mpingo yoyera ya Katolika, ndi zinthu zina zonse izi, ndi "Mulungu, Atate wamphamvu zonse, amene amasunga kumwamba ndi dziko lapansi," izo ndi zankutu. Uko nkulondola. Izo siziri mu Baibulo. Palibepo chinthu cha mtundu umenewo mu Lemba. Izi ndi zikhulupiriro zongopeka zimene iwo anazipeka, koma ndi Mapemphero onse ndi zina zonse ndi chinthu chongopeka.

Ife tikuwona lero kuti a chiprotestant athu awa pamene ife tifika muno, basi izo zinangowadutsa iwo. Ndipo monga momwe Billy Graham ananena Lamulungu, "Anthu akhala ali mu zoyipa kwambiri, mpakana pamene iwo akuganiza kuti iwo onse ndi okhoza, pamene iwo ali olakwitsa." Uko nkulondola. Ichi ndi choonadi. Ine ndiri wokondwa kuti ine Chifukwa, ine ndikudziwa Billy Graham analandira Mzimu Woyera pansu pa George Jeffries uko. Koma ena mwa masiku awa iye adzatulukamo m'menemo. Mulungu akumugwiritsa ntchito iye apo tsopano, chifukwa iye angagwedeze ufumu umenewo

umene palibenso wina, mwina, angalowemo. Koma inu mukhoza kuwona malalikidwe ake, kuti pali china chake kumbuyo kwake, chifukwa cha ena mwa awa a Baptisti ogwirana chanza. Inde, bwana.

59 Tsopano.

Ine ndikudziwa ntchito zako, ... ndi kudekha kwako, ... kuti iwe sungakhoze

Tiloleni ife tiwone tsopano, Ine ndiri ndi ...

Ine ndikudziwa ntchito zako, ndi kulemedwa kwako, ndi kudekha kwako, ... ndikuti sukhoza kulola oyipa; ndikuti iwe wawayesa iwo amene amazitchula okha atumwi, ndipo iwo siali, ndikuti iwe waapeza iwo abodza:

Iye anawapeza iwo kukhala abodza. Kodi iwo akanadziwa bwanji chimenecho? Iwo samayenda ndi Mawu. Tsopano, ngati munthu anganene kuti Baibulo iri likunena mu Aheberi 13:8, Yesu Khristu Yemweyo dzulo, lero, ndikunthawi zonse; ndipo munthu anati, "Awu! Masiku a zozizwitsa anapita," ndiyeno munthu ameneyo ndi wabodza.

Ngati Baibulo linati, "Lapani, ndipo batizidwani aliyense wa inu mu Dzina la Yesu Khristu kuloza kuchikhulukiro cha machimo anu," ndipo malo aliwonse mu Baibulo akunena chinthu chomwecho; ndipo wina aliyense amene anabatizidwapo mu nthawi ya Baibulo anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu; ndipo iye akuwatuma iwo kuti akabatizidwe, pokonkha, kapena china chake monga icho, munthu ameneyo ndi wabodza, iye wapezeka ali m'neneri wonyenga.

Ine ndikuyembekeza sindikuvulaza kumverera, koma, m'bale, inu simungathe kuchilera ichi. Ndi nthawi yoti tivule magolovesi ndikuwugwira Uthenga, mwaona. Icho ndi choonadi.

60 Tsopano, mudiwonetse ine china chake chosiyana. Mudiwonetse ine pamene munthu m'modzi anabatizidwapo mu njira ina iriyonse kupatula mu dzina la Yesu Khristu, mwaona, kunja kwa Mpingo wa Katolika.

Kotero, ngati inu mwabatizidwa mu njira imeneyo, simuli mu Mpingo wa chiKhristu; inu muli mu mpingo

wa chikatolika, chifukwa inu munabatidwa Mlendo wawo yemwe wa Lamulungu," katikisimu anati Funso, "Kodi ma Protestant adzapulumuka?"

Anati, "Ambiri a iwo, chifukwa iwo ali ndi ubatizo wathu ndi zinthu zambiri monga izo." Anati, "Iwo amadzinenera zokhudza Baibulo, ndipo Baibulo linati, 'Batizani mu Dzina la Yesu Khristu.' Ndipo ife tazichotsa izo m'menemo, ndikuyikapo, Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera,' ndipo iwo agwetseredwe pansu ku icho." Ndithudi.

Uwo siubatizo wa chiKhristu. Uwo ndi ubatizo wa Chikatolika. Kodi inu munandimva ine usiku wina, "Kodi inu munayamba mwabatizidwapo mu ubatizo wa Chikristu?" Ubatizo wa Chikristu - khristu, Yesu Khristu; osati mu udindo wina.

61 Tsopano, ndime ya 3 tsopano. Chabwino. Ndime yachiwiri ndi ya 3. Tsopano ndime ya 3:

Ndipo wanyamula, ndipo unali ndi kudekha, ndipo chifukwa cha Dzina langa walemedwa, ndipo sunakomoke.

"Chifukwa cha dzina langa." Kodi inu munazindikira iwo anali nako kudekha? Kulemedwera chani? Dzina Lake. Kodi inu mukuliwona Dzina ilo likugwiridwa mu Mpingo uwo? Tsopano chioneni icho, pamene ife tikudutsa kupyola mu sabatayi, m'mene icho chikuzilalira ndikupita mu dzina lina, mwaona. "Iwo anali ndi kudekha, kulemedwa, ndi zina zotero, ndipo chifukwa cha Dzina Langa." Iwo anavutika chifukwa cha Dzina Lake, kulisunga Dzina la Yesu Khristu pamwamba pa Mpingo uliwonse, pamwamba pa china chirichonse, liloleni ilo likhale loyamba.

"Chirichonse ...," Baibulo linati, "Chirichonse chimene inu muchita mu mawu kapena ntchito, zichiteni izo zonse mu Dzina la Yesu Khristu." Kodi uko nkulondola? Chirichonse chimene inu muchita mu mawu kapena mu ntchito. Ngati inu mukukwatitsa, mukukwatitsa munthu Ngati inu simungathe ... ngati iwo onse ali osokonezeka mu ukwati wawo, musawakwatitse iwo nkomwe, mwaona. Ngati inu simungathe kuyankhula

mwaufulu, kuti "Ine ndikukulengezani inu mwamuna ndi mkazi mu Dzina la Yesu Khristu," aloleni iwo apite. Chabwino. Ngati inu mukufuna kuwabatiza iwo, abatizeni iwo mu Dzina la Yesu.

62 Ngati inu mukuyenera kuchita chinthu china chake chimene inu simungathe kuchichita icho mu Dzina la Yesu, chisiyeni icho chokha. Wina wake anati, "Imwani pang'ono." Inu simungachichite icho mu Dzina la Yesu. Kotero chisiyeni icho chokha. Winawake anati, "Sewerani ma card pang'ono." Inu simungachichite icho mu Dzina la Yesu, kotero chisiyeni icho chokha. Nthabwala yaying'ono, yauve, yoyipa pa mphwando lanu Inu simungazinene izo mu Dzina la Yesu, kotero chisiyeni icho chokha, mwaona. Inu simungavale timakabudula mu Dzina la Yesu, kotero chisiyeni icho chokha.

Ine ndikanatha kupitiriza, koma inu mukudziwa kuti ine ndiyankhula zokhudza chiyani. Chabwino. Inu simungachite chimenecho ... chimene inu simungachichite mu Dzina la Yesu, chisiyeni icho chokha, chifukwa Iye anati, "Chirichonse chimene inu mungachite nu mawu kapena mu ntchito, zichiteni izo zonse mu Dzina la Yesu Khristu." Chabwino, tsopano.

63 Tsopano, ife tikupita ku Iye anawayamikira iwo pa icho.

Tsopano ine ndikhala ndikuyankhula zokhudza dandaulo tsopano inu mutu wa 4 ... kapena ndime ya 4, kani.

Koma ndiri nako kanthu kotsutsana ndi iwe, unataya chikondi chako choyamba.

O. "Ine ndiri nako kanthu kotsutsana ndi iwe. Iwe wakhala uli wodekha. Iwe wagwiritsitsa Dzina langa." Kodi icho sichingakhale basi chinthu chabwino kwa kachisi uyu lero? Inde, bwana. "Iwe wakhala uli wabwino. Iwe unali nako kudekha kwakukulu, ndipo wapirira kwanthawi yayitali. Koma chinthu cha icho ndichakuti Iwe wagwiritsitsa Dzina langa. Ine ndikuthokoza zonse izo. Ine ndikukuyamikira iwe chifukwa cha icho. Chabwino. Ndipo Ine ndawona kuti iwe unawayesa iwo amene amanena kuti ali atumwi,

ndi zina zotero, ndikuwapeza iwo abodza. Iwo sakugwirizana ndi Mawu. Ine ndikuyamikira zonse izo."

"Koma pali china chake chimene Ine ndiri nacho chotsutsana ndi iwe, ndipo chimenecho ndi ichi kuti iwe wasiya chikondi chako choyamba. Iwe unasiya chikondi chija chimene iwe unali nacho nthawi ina pa misonkhano ija ya bwino, yachikale, ya Mzimu Woyera, ndipo iwe unayamba kukhala ngati kubwerera m'mbuyo kupita ku mwambo uwo.... Kubweretsamo 'Atate wathu'" zankutu, mwaona.

64 Bungwe la anthu lonse iri liri pano, ndipo wina wake ndikutuluka ndi mkanjo wawukulu pa iwo, inu mukudziwa, kumayimba inu kwaya, inu mukudziwa; ndi tsitsi lawo lonse loyikidwa mankhwala, ndi chirichonse, ndi nkhope zawo zopenta; ndipo iwo nkumayimba ngati ine sindikudziwa chiyani.

Pano osati kale, ngati iwo siunali msonkhano wa Oral Roberts, ine ndikutsimikiza ndikayitanira gulu ilo panja. Ine ndinali pa msonkhano wa amuna a zamalonda, iwo umachitikira ... Ife tinalibe ... usiku umenewo ine ndimayenera kuti ndiyankhule. Iwo sakanatha kuwuchititsa iwo mu hotela, ndipo iwo ananditengera ine kunyumba ya Oral Roberts.

Ndipo pamene ine ndinakhala mowerengera mwa Oral, apo panali gulu la ana achipentekosite - o, amuna ndi akazi aang'ono, azaka khumi ndi zisanu ndi chimodzi, khumi ndi zisanu ndi ziwiri, zakubadwa, khumi ndi zisanu ndi zitatu, onse atayima apo kunja uko, amene anali pakati pa makumi atatu kapena makumi anayi a iwo - akupita kukayimba china chonga ... zimene kwa ine zimamveka ngati china chake chongosangalasa ngati chimene Becky anayankhula za icho, Tchaikovsky, kapena china chake chofanana ndi chimenecho. Ine sindikudziwa - zina mwa nyimbozo, zokhala ngati nyimbo za, nyimbo zachikunja zachikale. Ndipo iwo anali pamenecho.

Ndipo abale amakatolera chopereka mu msonkhano. Ndipo aliyense wa awa anamutsatira iye ndipo iwo anali ndi kakapu kakang'ono, nkumachita ngati anali akhungu. Ndipo ndi nthabwala zonse, ndi kutengeka, inu munayamba mwamvapo, pakati pa iwo anyamata ndi atsikana, ndikuyankhula ngati chirichonse. Ndipo iwo atsikana atazipaka

penti yokwanira paiwo, yomwe akanatha kupenta nayo pafupifupi nyumba ya Oral. Ndipo apo iwo anali ngati chimenecho, ndikumadzitchula iwo okha a Chipentekosite. Iwo anataya chikondi chawo cha poyamba.

65 Ine ndithudi ndikugwirizana ndi David Duplessis, "Mulungu alibe zidzukululu." Ayi, bwana. Ife tiri ndi zidzukululu za Methodists ife tiri ndi zidzukululu za Baptist, ife tiri ndi zidzukululu za Chipentekosite; koma Mulungu alibe. Inu ndinu ana amuna ndi akazi. Inu simungalowe kudzera pa mayi wanu kapena bambo wanu, chifukwa iwo anali amuna ndi akazi abwino. Inu mukuyenera kupereka mtengo womwewo umene iwo anapereka. Inu mukuyenera kuti mubadwe mofanana ndi m'mene iwo anabadwira. Mulungu alibe zidzukululu ngakhale pang'ono. Inu ndinu mwana wa mwamuna kapena wa mkazi; kapena inu sindinu chidzukululu. Icho ndi chinthu chokhacho.

66 Tinapita ku msonkhano uko, tchalitchi chabwino cha Pentekosite Assembly. Mnyamata, mukanawona azimayi awo akumwazikana pamene iwo anandiwona ine ndikulowa - ndi tsitsi lawo lodula iro, ndi awo aang'ono a kale ... ovala mwatheka, ngati soseji, pafupi - fupi, inu mukudziwa, kuwonetsa khungu lawo mu madiresi awo monga choncho, - akazi a Chipentekosite, ovala mochititsa chigololo. Inu mukayankhira izo pa tsiku la chiweruzo. Inu mukapezeka olakwa pa mlandu wochita chigololo. Yesu anati, "Wina aliyense woyang'ana pa mkazi ndikumusirira iye wachita chigololo ndi iye mu mtima mwake kale." Ndipo ngati inu mukudzipereka nokha kwa amuna monga choncho, wochimwa ndi ndani? Ndi inu, kapena mwamuna?

Mukhale olongosoka. Pewani maonekedwe ali wonse a tchimo ndipamenepo.

67 Kodi inu mukanachita chiyani? Anataya chikondi chawo choyamba.

O, inu simukanatha kuwapeza iwo ali pa ngodya ndi chisakasa kuwomba m'manja ndi kulemekeza Mulungu. O, ayi. Iwo amayimba china chake chofanana ndi china chake chachikunja chachikale, ndi mulu wa mikanjo yovekedwa pa iwo. Mwaona, iwo anataya chikondi chawo choyamba. Ilo ndi limene liri vuto ndi Mpingo woyamba, mwaona. Iwo basi amangochita ngati dziko.

Iwo amayenera kuvala ngati dziko, kuwoneka ngati dziko, kuchita ngati dziko, ndikukhala naye katswiri wawo wa pa television womukonda, inu mukudziwa. Iwo sangasiye kumuwona iye, "Ife timamukonda Suzy," kapena winawake, inu mukudziwa. Iwo basi akungoyenera kuchiwona icho. Iwo amakhala kunyumba m'malo mopita ku msonkhano wa mapemphero, ndi china chirichonsecho, kuti awone icho. Ngati iwo sachita icho, iwo azimuzuma m'busa wawo, kuti awalole iwo kutuluka mwamsanga mpakana pologalamuyo ibwerapo, koteri kuti iwo akafike kunyumba kuti athe kuyiwonera iyo. Chikondi cha dziko koposa chikondi cha Mulungu!

O, zamwambo kwambiri. Inu simunganene kuti, "Ameni" naponso. Mayo ine, icho chikanaphwasula zina za zophodaphoda, mwaona. Iwo alibe icho ayi Awo ndi a Pentekosite. Awo si Abaptist. Iwo sanayambe akhalapo nacho icho kuyamba ndi kuyamba ... Achiprezibateria. Ine ndikuyankha zokhudza a Pentekosite. Uko nkulondola.

Ine ndikudziwa izo ndi zodwalitsa koopsy m'bale. koma ife tikufuna kubadwa kutuluka ku chinthu ichi. Chiyenera kubweretsa imfa pasanakhale kubadwa. Icho ndi choonadi. Koma ndi inu muli apo. Kusiya chikondi chanu choyamba.

68 Ngati Mulungu anali nacho icho chotsutsana ndi Mpingo uwu, Iye ali nachonso chotsutsana ndi uwonso. "Chifukwa inu munasiya chikondi chanu choyamba. Ine ndiri nacho chokutsutsani inu. Ine ndiri ndi china chake chotsutsana ndi inu. Ilo ndiro dandaulo Langa. Inu munakhalapo nayo nthawi yayikulu, koma inu munayamba kulilola dziko kuyamba kukwawira mkati, ndipo inu munayamba kuchita ngati mwa mwambo pang'ono. Inu mudakagwirabe dzina langa, ndipo inu mudakachitabe zinthu zimene ndizolondola,

ndipo inu muli ndi kudekha kochuluka ndi zina zotero. Ndipo inu mukulemedwa ndi kugwira ntchito... muli ngati mule. Inu mumangolemedwa ndi kugwira ntchito."

Kalanga, Kalanga, Kalanga ine! Mwaona, inu mwachisiya chisomo, ndi chikhulupiro ndi mphamvu, kuchisinthanitsa icho ndi kulemedwa komanso zintchito. "Chabwino, ine ndikukuwuzani inu M'bale Branham, ine ndimathandiza mkazi wamasiye wina aliyense amene ine ndingathe."

Chabwino, icho ndi chinthu chabwino. Ine ndi kukuyamikirani inu chifukwa cha chimenecho. Koma chiri kuti chikondi chanu choyamba chija chomwe inu munayamba mwakhalapo nacho? Chiri kuti Chimwemwe chija chimene inu munkakhala nacho? Monga Davide analirapo nthawi yina, "O Ambuye mubwezeretse kwa ine chimwemwe cha chipulumutso changa." Mwaona. Kodi irikuti misonkhano ija ya mapemphero a usiku wonse, ndi misonzi mumasaya mwanu?

Mayo ine! Baibulo lachitanso fumbi, ndipo liri ndi akangaude pa ilo. Inu mumawerenga nthano za chikondi zakale, ndi nkhani, ndi zinthu - ndi zinthu zomwe sizinayenera kuloledwa nkomwe kuti zikasindikizidwe koma kuponyedwa ku chitini chazinyalala. Ndipo ife anthu aChipentekosite tikuzitenga zimenezo, ndipo basi ndikumasangalala nazo, ngati mulu wa ntchentche pa chitini chazinyalala. Uko nkulondola. O, chifundo!

Chimene ife tikusowa ndi kubwerera ku chikondi chatu choyamba, kubwerera ku Pentekosite. Ndibwino ine ndichoke pamenepo. Chabwino, koma inu mukumvetsetsa kusiya chikondi choyamba icho.

69 Ndime ya 4, ndime ya 5 tsopano. Chenjezo, ndime ya 5, chenjezo: kumbukira ndipo ulape, mwaona.

Choncho kumbukira kumene iwe wagwerako [Kodi iwe Unachokera kuti? Kuchokera ku Pentekosite iwe unagwera kumene iwe uli tsopano, kubwerera m'mbuyo], ndipo ulape, ndipo uchite ntchito zako zoyamba [Bwaereranso ku Pentekosite kachiwiri]; kapena Ine ndidzadzaza kwa iwe mwansanga, ndipo Ine ndidzachotsa choyikapo nyali chako kuchichotsa pa [A - k - e ... kuwona chimene Iye ali, sichoncho inu?] malo ake, kupatula iwe utalapa.

Mawu ena, ngati inu mutakhala ndi m'busa wodzazidwa, ndi Mulungu, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo inu mukuyesera kumutengera iye ku chala chanu, ndikuti, "Chabwino, ngati iye anganene chirichonse chakudza ife kukhala ndi kwaya yovala mikanjo Ngati iye anganene chirichonse chokhudza ife kuvala zozipaka kumaso, ife basi tidzangomuchotsa iye." Inu musadandaule, Mulungu adzachichita icho inu

musanapeze mpata kuti mutero. Iye adzatuluka ndi kukalalikira ku miyala pa msewu iye asanayambe wanyengerera zinthu za mtundu umenewo. Inu muli ndi m'busa amene mwamtheradi akukuwuzani inu choonadi, inu mukuyenera kulemekeza Mulungu, ndipo mukhale mu Mzimu, ndikupembedza Mulungu, ndi kuzindikira kuti inu mungatayike ngati inu simutero, mwaona.

70 Koma anthu akukhala lero ngati ichi ndi chinthu chokhacho chimene chinalipo, kukhala pano pa dziko lapansi, chokhacho basi. Inu simukuzindikira kuti inu muli ndi solo imene idzachoke pano, ndikupita kwina kwake. Ndipo inu mumasindikiza kopita kwanu pompano, njira yomwe inu mukukhalira moyo, ndi njira yomwe inu mukuchitira. Kusunga mkwiyo, ndi kuuma mtima, ndi chirichonse - ndipo kenako kuthamangira ku tchalitchi. O, chifundo! Psyfuu! Manyazi pa inu. Inu mumabweretsa chitonzo pa cholinga cha Khristu. Kodi uko sikulondola? Kodi ife sitimachita izo?

Mbiyang'ambe sakuvulaza Mpingo. Sichimenecho ayi. Si hule amene akuwuvulaza Mpingo. Ndi anthu amene amalengeza kuti iwo ndi akhristu amene akuwuvulaza Mpingo. Ife tikudziwa chimene mbiyang'ambe ali ndi chimene hule ali. Pamene alongo athu avala ngati hule, icho ndichosiyana. Chimenecho ndichimene chikuwuvulaza Mpingo. Pamene munthu amwa ngati mbiyang'ambe, chabwino, ndiyeno, chimenecho ndichimene chikuwuvulaza Mpingo. Iwo amalengeza kuti ndi akhristu, ndipo kenako iwo amachita chimenecho.

Anthu amakuyang'anani inu dzina limenelo "Muloleni iye amene ngakhale amatchula Dzina la Yesu Khristu achoke pa tchimo," mwaona. Chokani ku ilo. O, ife ndi operewera kwambiri, abale. Ine, inu, ife tonse. Ife ndi operewera ku chimene Khristu akufuna kuti ife tikhale. Ndipo pano mutsiku iri ndi nthawi yoti tiyike pambali tchimo lina liri lonse limene limatisautsa ife mosavuta, ndikuthamanga modekha mpikisano umene wayikidwa pamaso pathu. Alaliki, uko nkulondola, abale. Uko ndi ndendende kulondola.

71 "Kumbukira ndipo ulape, kapena Ine ndidzachotsa kuwala kwa nyenyezi kukuchotsa pamalo pake." Kodi malo akewo ndi chiyani? Mutchalitchi. "Koma ngati iwe sulapa, ndikubwerera kumene unali poyamba, Ine ndidzachotsa m'busa wako kuchokera

kwa iwe. Ndi kumusuntha iye kuchoka pa malo pake. Ine ndidzamuyika iye pena pake pamene wake... pamene Ine ndidzawonetsa kuwala kwanga kumene kudzawala." Kodi izo sizinali zosimidwitsa?

Ndi nthawi yoti Mpingo ilape. Ndi nthawi yoti a Pentekosite achotse masikolala aang'ono ochuluka

opukutidwa awa kuwachotsa m'maguwa, ndipo atenge wolalikira wachikale ndi kumuyika pamenepo amene adzakuwuzeni inu choonadi; osati kukusisitani inu ndi kumawugwiritsa ntchito Mpingo kuti apeze tikiti ya chakudya, malipiro aakuru, ndi china chake monga icho; ndi maphunziro a zaubongo, ndi mipikisano yochepa ya hatchi, ndi maphwando a madzulo a misuzi ndi china chirichonsecho. Ndi nthawi yobwerera ku Uthenga.

Ine sindikusamala kuti kaya ndinu ochepa motani. "Pamene awiri kapena atatu asonkhana, Ine ndidzakhala pakati pawo." "Lapani, koma ngati sutero Ine ndibwera ndikudzachotsa choyikapo nyali; kumutumiza iye kutali, kapena ... basi kungowalitsa nyali zake."

72 Tsopano ndime ya 6. Tsopano pano pali Imodzi Imene ife tikhale nayo pamavuto. Tsopano, kupatula inu mutalapa Iye adzabwera ndikumuchotsapo m'busa.

Koma ichi iwe uli nacho, ...

Tsopano, kumbukirani. O, musachiphonye ichi tsopano. Ichi chikhala kutsekera zina zonse pamodzi, kutsika mpaka ku m'badwo uno umene ife tirimo tsopano. Wina ali yense kumverera bwino poyamba? [anthu osonkhana anena, "Ameni,"] Kodi inu muli pa changu? [Osonkhana anena, "Ayi."] Chabwino tsopano. Chabwino. Mungopirira basi pang'ono pokha ndiyeno. [M'bale mwa anthu osonkhana anati, "Tikhale usiku onse."] Tsopano ndikukuthokozani inu.

Koma ichi iwe uli nacho... 1. [NdIyeno iwo anali ndi chinthu china, kodi iwo sanali? Tsopano kodi iwo anali ndi chiyani?] ... kuti iwe udana nazo ntchito za aNikolayi zimene inenso ndidana nazo.

"Iwe ukudana nazo ntchito izo za aNikolayi" Nditakhala mowerengera lero kumtunda uko ine ndinalamba china chake apa pa zimenezo. Ine ndikufuna inu mumvetsera mosamalitsa tsopano. Icho chiri pamasamba angapo pano. Ndime ya 6 ikutamanda, ndipo ikuvomereza. Uyo ndi Mulungu ndi Mpingo kugwirizana pa chinthu chimodzi, kuti iwo anadana ndi zintchito za a Nikolayi. Mpesa woona ... mpesa woona, Mpingo woona umene unali mu Mpingo wa Aefeso uwu....

73 Tsopano, kumbukira, Mpingo uliwonse uli ndi miyambo yake, ndipo Mpingo uliwonse uli ndi zauzimu zake. Awo ndi mapasa amene amabadwa mu chitsitsimutso chinachirichonse, ndikukhala mu mpingo uliwonse. Iwo anachiyamba icho mu m'badwo uwu ndi kukathera mu m'badwo uwu; Ndipo pamapeto pake amiyambo anachitenga icho kupita mu m'badwo wa Tiyatira, ndipo Luther anachikokeranso icho m'mbuyo kachiwiri. Ndipo tsopano icho chikuzungulira mobwerera kuti chilowe mkati kachiwiri.

Kodi inu mukuchiwona chipembedzo cha mwambo icho? Palibe kusiyana pakati pa chimenecho ndi chikatolika. Icho chonse ndi chinthu chimodzi. Bungwe lina liri lonse likuphedwera mu icho. Mulungu sanapangapo bungwe Mpingo wake. Ichi ndi ndendende chimene iwo amayesera kuti achite apa, ndipo inu penyani ndipo muwone, tsopano, ngati icho sichiri kulondola. Basi kungokuwonetseni inu m'mene bungwe liriri lotembereredwa. Icho chinali chachilendo ku Mpingo watsopano, Mpingo wa chipangano chatsopano, , mwaona.

74 Koma ichi iwe uli nacho, kuti iwe udana nazo ntchito za aNikolayi, zimene inenso ndikudana nazo.

Mpesa woona kudana ndi ntchito za mwambo za aNikolayi. Kotero Mulungu nayenso anadana nazo. Zimene zinali ntchito mu Mpingo wa Aefeso, mu Mpingo wa Aefeso, zinakhala chiphunzitso mu Mpingo wa Pergamo. Mu Efeso, Mpingo woyamba, iyo inali ntchito. Mu Mpingo wotsatira icho chinakhala chiphunzitso. Kodi inu mukuchimva chimenecho? Kodi inu mukuchimvetsetsa icho tsopano? Icho chinali ntchito mu Efeso. Ndipo penyani. Cha apa mu Pargamo Chinakhala chiphunzitso. Icho basi chinayambika

apa mumawonekedwe ochepa amwana. Tsopano, mukamphindi ife tikhala tikufufuza chimene icho chinali. Pano pali "ankhandwe," aPaulo, ntchito za aNikolayi.

75 Tsopano chiyani ... Tiyeni ife tilisanthule liwu limenelo, tipeze chimene ife tinali nacho ife tisanapite patali. Mawu akuti "Nikolayi" ndi ngati chinthu cha chilendo kwa ine. Ine ndinapeza dikishonale ya chi Greek imene ndikanatha kuyipeza. Nikolayi anachokera ku mawu a "Niko," N - I - C - K - O -. dikirani, ndi kukhulupirira ine ndinachilemba icho apa. N - I - C - K - O, "Niko," chimene chikutanthauza "Kugonjetsa, kapena kuchotsa paulamuliro, kapena kugonjetsa, osonkhana.

Chimene iwo amayesera kuchita apa chinali kuyesera kuwutenga Mpingo kumene Mulungu anali ndi azibusa, ndipo Mzimu wa Mulungu akuyenda ndi mphatso mu Mpingo wa Mulungu wamoyo; ndipo iwo anali ndi chiphunzitso chimene chinayambika kuti iwo ayambe kukhala ndi ansembe, ndi mabishopu, ndi ma papa, ndi ena otero, chimene Mulungu ananena kuti Iye akudana nacho. Iye akudana nacho icho ngakhale lero. Chinikolayi - "Niko," kugonjetsa kapena kuchotsa pa ulamuliro anthu osonkhana.

"Anthu osankha" ndi Mpingo. Ndiangati amene akudziwa kuti anthu osonkhana ndi Mpingo?

76 Chabwino. "kuchotsa pa ulamuliro, kapena kugonjetsa, kapena kutenga malo a wanthu osonkhana." Mu mawu ena, kutenga zonse za kupatulika, mphamvuzonse zochokera mu Mpingo, ndikuzisiya izo pa

ansembe. Aloleni osonkhana adzikhala mu njira yomwe iwo ukufuna, koma wansembe ndiye woyera. Kuwuchotsa Mzimu Woyera mwa anthu ndi zizindikiro ndi zozizwitsa zikuwatsata iwo, ndi kuuchotsamo iwo ndi kuwapatsa iwo unsembe woyera; kuchotsa Mzimu Woyera, ndikuwusinthanitsa iwo ndi unsembe.

Inu mukuwona chimene icho chinali? Icho unali Icho chinali.... ichoo pomapeto pake chinakhala Mu Mpingo uwu apa; iyo inali ntchito; ndipo pa malo awa icho chinakhala chiphunzitsa; ndipo mu Tiyatira, icho chinalowa m'malo. Ndipo pamene Luther anatuluka, icho sichinatha kukhala njira yomweyo. Icho chinabwerera m'mbuyo, ndikudzalowanso m'malo kachiwiri - mabishopu, makadinolo, mabishopu akulu. Kodi ndi

ndani mu dziko lapansi amene ali mtsogoleri wa Mpingo wa Mulungu koma Iye Iyemwini? Amen. Psyyuu! Tsopano ine ndikumverera chipembezo.

Mzimu Woyera unatumizidwa kuti udzalamulire Mpingo. Osati basi mlaliki yekha; osonkhana wonse. Basi wolalikira yekha kukhala woyera; ndi Mpingo wonse kukhala nawo Mzimu Woyera. Ndipo m'malo mwa icho, m'malo mokhala nawo Mzimu kuchichita icho, iwo atenga bisiketi yaying'ono, yopyapyala, ndi mabisiketi owuma, ndi vinyo, ndikuzitchula izo ukalisitiya woyera, zimene zimatanthauza Mzimu Woyera.

Ndi zotheka bwanji pa dziko lapansi pamene bisiketi louma ndi vinyo zingakhale Mzimu? Tsopano, ngati izo ndi choncho, inu mukuyenera kuwerenga Machitidwe 2 monga chonchi: "Pamene tsiku la Pentekosite linabwera mokwanira, apo panabwera wansembe wa chiroma kumtunda mu msewu, ndipo iye anati, 'Tulutsani kunja lilime lanu.' Ndipo iye amayala bisiketi yopyapyala pa ilo, ndipo iye anamwa vinyo. Anati, 'Tsopano iwe uli ndi Mzimu Woyera.'"

Tsopano ife tikuganiza kuti icho ndi choopsa. Icho chiri.

77 Tsopano tiyeni titsike kumusi Ine ndinadzozedwa mu Mpingo wa Baptist. Tiyeni tiwatenge ife a Baptisti, a Methodist. Kodi ife timachita chiyani? "Ngati inu mudzavomereza kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu inu mwapululumutsidwa." Mdierekazi amakhulupirira kuti iye ndi Mwana wa Mulungu, ndipo amanjenjemera ku icho, chifukwa iye akudziwa kuti wathedwa.

Tsopano ife tichitenge icho mu mawonekedwe achiMethodist. Iwo amanena kuti Yohane sanabatize; koma iye amawakonkha. Anati panali minjale yambiri mu dzikomo ndipo madzi amakwera m'malomo. Ndipo iye anali ndi kachigoba ka nkho ndipo iye anaboola mphanga mu njale. Ndipo iwo kwenikweni amalalikira zimenezo. Ndipo iwo anali ndi madzi mu njale iyi kapena mu chigoba chankhono kunja kwa mphanga ya njale, ndipo amawakonkha anthu. Zamkutu! O, m'bale!

78 Chabwino, pano ife tichitenge icho. "Pamene tsiku la Pentekosite linabwera mokwana iwo anali pa malo amodzi mu cholinga chimodzi. Ndipo m'busa anatsika

nalalikira ulaliki wabwino, ndipo anati; 'Mundipatse ine mkono wa manja wa chiyanjano, ndipo ife tidzalemba dzina lanu mu buku.'

Icho sichikumveka bwino. Icho chikutero? Inu mwina mutha kuchipeza icho... inu simukanatha kuchipeza icho mu alamanaki. Iwo amadziwa bwino kwambiri koposa chimenecho. Tsiku lobadwa la madona akale achi alamanaki ndilolondola kwambiri koposa chimene icho chikanakhala.

Chabwino, ndiyeno chimene chinapangitsa icho ndi chiyani? A Chinikolayi kubweretsamo gulu la azibambo kuti apotoze Lemba, ndikupanga chipembedzo chimene sichingamulole Mulungu kuyenda mu icho. Kuferatu pomwepo. Ndichifukwa chake Iye anati pano, "Inu ndinu akufa. Inu muli ndi dzina loti muli ndi moyo, koma ndinu akufa." Ambiri a iwo ndi akufa, ndipo osachizindikira icho.

79 Ine ndi m'bale wanga timawedza pamene ife tinali anyamata ang'ono pamtunda apa, ndipo ine ndinagwira Kamba woluma wokalamba. Ndipo ine ndinadula mutu wake, kumuchotsa pa chingwe (sindimafuna kupusa ndi chinthu icho), ndikuponyera iye pamtunda uko. Ndipo m'bale wanga wang'ono anatsatira, ndipo iye anati, "Kodi iwe unagwira chiyani kanthawi kapitako?"

Ine ndinati, "Kamba."

Iye anati, "Kodi iwe unachita naye chiyani?"

Ine ndinati, "Uyo, wagona apoyo, ndipo mutu wake ndi uwo wagona apowo."

Ndipo iye anapita pamenepo, ndipo iye anati, "Kodi iye wafa?"

Ine ndinati, "Ndithudi. Mutu wake walekanitsidwa ndi thupi lake. Akuyenera kuti wafa."

Kotero iye ananyamula kandodo ndikuyamba kukankhira mutu wa kambayo kuwubwezera mu mtsinje, kukamtsinje kakang'ono. Ndipo pamene iye anachita, Kamba wokalambayo anachigwira icho. Inu mukudziwa iwo adzaluma kwa ora limodzi kapena awiri. Iye adumpha mobwerera mbuyo.

Iye anati, "Hei, ine ndimaganiza iwe unanena kuti iye ndi wakufa."

Ine ndinati, "Iye ali."

Iye anati, "Chabwino, iye sakudziwa icho." Kotero, umo ndi momwe anthu ambiri aliri. Akufa koma osachizindikira icho.

A Nikolayi. O, kalanga ine! O, Iye anati, "Iwe ukudana nacho." Kutenga zonse za ... ansembe abwino oyera, makadinolo oyera, mabishopu oyera.

80 Ndipo ena a inu achipentekosite, "Oyang'anira wamkulu, muloleni iye atsike. Oyang'anira wa wa onse, iye adzakuwuzani inu kuti mukhala nawo msonkhano wa machiritso kapena ayi." Aleluya! Mzimu Woyera ndi yekhayo woti anene chimenecho kapena ayi. Ndi Mawu a Mulungu a muyaya.

Chabwino, M'bale Branham, ife timakhulupirira kuti Baibulo limaphunzitsa ubatizo mu Dzina la Yesu, koma oyang'anira wa onse anati ife tikachiyamba chimenecho mu Mpingo wathu iye adzatiponyera ife tonse kunjani. Pitirizani. Uko nkulondola. Ndikwabwino ine ndiponyeredwe kunjani pano kuposa kukaponyeredwa kunjani uko. Kotero, ngati inu muchotse china chake pano, inu mukaponyeredwa kunjani kumeneko muli monsemo. Kotero inu mukuyenera kuti inu muponyeredwe kunjani pompano. Ngati iye akukankhireni kunjani pano inu mukakankhiridwa mkati uko. Kotero, icho basi ndi chinthu chofanana. Kotero, khalani mowongoka ndi icho.

Ife tikufuna tikhale olondola. O, kalanga ine! Ichi ndi chinthu chofunikira kwambiri, m'bale. ife tikuyenera kuchipeza chinthu chimenecho molondola. Ife sitizakhoza kukhala nawo Mpingo mpakana Mulungu atapeza maziko oti uyalidwepo. Iye sadzamanga nkomwe Mpingo wake pa gulu la zamkutu. Iye akuyenera kubwera pa Mawu Ake, kapena Iye osabwerapo nkomwe - molunjika pa Mawu Ake.

81 Wina wake osati kale kwambiri kumtunda uko anati, "M'bale Branham, tulukani ku Chatauqua." Ndiangati amene anali ku Chatauqua? Chabwino, basi mungoyang'ana kuno - anthu ochuluka gawo limodzi mwa magawo atatu amu Mpingo anali ku Chatauqua. Tsopano mwamuna uja anayimirira madzulo aja kumene kuja, ndipo inu nonse

munamumva iye - osazindikira kuti ine ndikudziwa zokhudza icho. Mulungu akhoza kuwulula mu chipinda kumtunda uko zimene iwo akuyankhula kumusi uko, ndipo inu mukudziwa kuti iye anachichita chimenecho.

Kubwera kumtunda uko, anati, "Tsopano, M'bale Branham, O, iye, ndi mtumiki wa Ambuye. Pamene Mzimu ukhala pa iye, iye ndi Mneneri wodzozedwa. Iye amadziwa motsimikizika... Mulungu amamuwuzwa iye chimene icho chiri, ndi chimene chikhalepo. Koma maphunziro ake a zaumulungu, osamamvetsera ku chimenecho."

Ilo ndi lingaliro losokonekera bwanji! Munthu angayankhule zimenezo motani Bwanji, ine sindina Chabwino, ngati inu simumadziwa kusiyantsa nyemba kuchokera ku khofii, inu mudzazindikira bwino kwambiri kuposa icho. Inu mungathe bwanji kulingalira za chinthu ngati chimenecho? Ndi chifukwa chiyani? Bwanji, mawu omwewo "mneneri" pa iwo wokha amanthauza wowulula wa Umulungu wa Mawu. zingatheke bwanji inu? "Liwu la Ambuye linabwera kwa Mneneri." Ine sindinanene kuti ine ndinali. Iwo anatero.

Koma ndinu apo, mwaona.

82 Momwe munthu ... kugwira kachiphunzitsa ka Mpingo penapake, chifukwa bungwe lawo silingagwirizane ndi icho, kugulitsa ukulu wanu chifukwa cha msuzi wa nyemba. Esau iwe wachinyengo womvetsa chisoni (uko nkulondola), kugulitsa ukulu wako chifukwa cha msuzi wa nyemba, chifukwa cha msuzi wa wachipembezo, msuzi wa bungwe limene Mulungu amadana nalo. Basi tangokumbukirani, inu mukuti bungwe? Mulungu amadana nalo ilo. Icho ndi chinthu chimene chinalekanitsa abale, ndipo chinaphwasuka....

Pano pali a Methodist, Baptist ndi a Presbateria ambiri usiku uno, amene akufuna kuti akhale ndi chiyanjano kuzungulira gome la Mulungu. Koma ngati iwo angatero, iwo adzakankhiridwa kunjani nthawi yoyamba pamene iwo oyamba mu icho. Uko ndi ndendende kulondola. Amai anali a chimenecho, ndipo iwo basi angokhala chidzukululu kuyamba ndi kuyamba. O, kalanga ine! Ine sindikusamala chimene amai anali. Amai

amakhala mukuwala konse kumene iwo anali nako mu tsiku lawo. Inu mukukhala mu tsiku lina.

83 Sayansi nthawi ina inatsimikizira, zaka pafupifupi mazana atatu zapitazo, pozunguliritsa mpira kuzungulira dziko, anati, "Ngati galimoto lirilonse lingayende pa liwiro lowopsa la mamailo makumi atatu pa ora; kukoka kudzalinyamula ilo padziko lapansi, ndikulitengera ilo m'malere." Inu mukuganiza kuti sayansi lero imakhulupirira chimenecho? Iwo akuthamanga mamailo mazana khumi ndi asanu ndi anayi pa ora limodzi. Iwo sakuyang'ana m'mbuyo kuti awone chimene iwo anachiyankhula; iwo akuyang'ana m'mbuyo

... kuti awone chimene iwo angathe kuchiwona poyang'ana kutsogolo.

Koma Mpingo nthawizonse umafuna kuyang'ana kumbuyo, kuwona chimene Wesley anayankhula, chimene Moody anayankhula, chimene Sankey anayankhula. "Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira." - Tiyeni ife tidziyang'ana kutsogolo! Chinthu chokhacho mu Baibulo chinayang'ana kumbuyo ...

Kodi inu mukudziwa kuti ndi nyama ya mtundu wanji imene nthawi zonse imayang'ana kumbuyo? Moyo wotsikitsitsa uli pamene. Ndiangati amene akudziwa kuti ndi moyo wotsikitsitsa chotani umene ulipo kwa iwo amene akuyenda? Chule. Chule ndi moyo wotsikitsitsa umene ulipo, ndipo munthu ndi moyo wokweretsetsa umene ulipo. Ndipo chule amayang'ana kumbuyo.

Ine sindimawukonda moyo uwo wapansi wachikale. Ine ndimafuna ndiziyang'ana kutsogolo, kukhulupirira, kudalira, kuyenda mu kuwala monga Iye ali mukuwala, (Ameni!), monga Iye akunyezimiritsa kuwala.

84 Nthawi yina uko ku Kentucky ine ndinali ndi msonkhano. Mamuna wokalamba anatuluka, ndipo anati, "O, ine sindimawakhulupirira machiritso amenewo."

Ine ndinati, "Chabwino, izo ziri bwino. Iwe ndi wa Chimereka."

Iye anati, "Ine sindimakhulupirira chirichonse pokhapokha ine nditachiwona icho."

Ndipo ine ndinati, "Chabwino, izo ziri bwino."

Iye anati, "Tsopano, ine ndiribe chirichonse chotsutsana ndi iwe, koma ine sindimakukhulupirira zimene iwe ukuziyankhula."

Ine ndinati, "Uwo ndi mwayi wanu wa chi Amereka. Inu mukhoza kusatero."

Iye anati, "Ine sindimavomereza chirichonse pokhapokha ine ndichiwone icho bwinobwino."

Ine ndinati, "Chabwino, izo ndizabwino. Inu mukuyenera kuti mwachokera ku Missouri."

Anati, "Ayi, ine ndine M'kentucky."

"Simukumveka mwabwino mwa uKentucky," Ine ndinati, "Koma muli monsemo," Ine ndinati, "Ngati m'menemo ndi momwe inu mukuganizira, inu pitirizani." Ndipo iye anati ... Ine ndinati, "Kodi inu mupita bwanji kunyumba?"

Iye anati, "Ine ndipita kudutsa Phiri. Ine ndi makhala Chabwino, mupita ndi ine." Mwamuna wabwino, Ananti, "Mupite ku nyumba ndi ine, mukhale usiku wonse, M'bale Branham."

Ine ndinati, "Ine ndikanakhumba nditatero, m'bale, koma," Ine ndinati, "Ine ndikupita kumtunda uko kwa amalume anga." Ndipo iye anati ... Ine ndinati, "Inu mukufuna mutakwera?"

Anati, "Ayi. Ine ndikuyenera kudutsa Phiri kumtunda uko, kumtunda njira iyi, ndipo kumusi dzenje, ndipo kumtunda" Inu mukudziwa momwe ziriri kumusi uko.

Ndipo Ine ndinati, "Chabwino," Ine ndinati, "Inu mukafikako bwanji kumeneko?"

Iye anati, "Ine ndikwera njira iyi uko."

"Bwanji," Ine ndinati, "Inu simungathe kuwona ngakhale dzanja lanu pamaso panu." Ine ndinati, "Inu mukafika bwanji kumtunda uko?"

Anati, "Ine ndiri ndi nyali."

Ndipo Ine ndinati, "Chabwino, kodi inu mumachita chiyani, kuyatsa nyali imeneyo, ndipo kenapo inu ndikumayenda ndi iyo?"

Iye anati, "Inu simungathe kuyiwona iyo."

Ine ndinati, "Ndiyeno inu mukafika bwanji kumeneko?"

"O" Iye anati, "Ine basi ndidzangoyatsa nyali, ndipo monga ine ndikuyenda, ine basi ndiziyenda ngati kuwala"

Ine ndinati, "Icho basi ndichimenecho. Ameni. Ndichimenecho. Basi kumangoyenda mu kuwala."

85 Basi muzingoyenda. Musangoyima chete - inu simungakafike kulikonse. Ngati inu mwawomboledwa, yendani mukuyeretsewa.

Inu mukuti, "Inu mungafika bwanji kumeneko?"

Basi muzingoyenda.

"Kodi Ubatizo wa Mzimu Woyera umachitika pambuyo pa kuyeretsewa? Kodi Ine ndingachipeze bwanji chimenecho?"

Basi inu muzingoyenda mukuwala.

"Kodi zizindikiro, zodabwitsa ndi zozizwa ...?"

Basi inu muzingoyendabe mukuwala. Muzingopitirizabe. Nthawi iri yonse inu mupanga sitepe, kuwala basi kuzadumphanga pang'ono chapatsogolo panu, chifukwa Iye amakhala patsogolo panu nthawi zonse. Iye samakakha; Iye amatsogolera. Iye ndi kuwala. O, ine ndine wokondwa chifukwa cha icho. Kodi inu simuli? Iye ndi kuwala; mwa Iye mulibe mdima.

86 "Iwe umadana nazo ntchito za Anikolayi." - Kukhala chiphunzitso.

Tsopano tiyeni tiwone chimene Paulo Tsopano, Mpingo wa ndani Kodi amene anayambitsa Mpingo umenewu ndi ndani tsopano? Paulo, Aefeso. Tiyeni titembenzire m'mbuyo tsopano ku Machitidwe, mutu wa 20 mu Kamphindi, mu

Machitidwe mutu wa 20, ndipo tiwone chimene Paulo Kodi inu mukukhulupirira kuti Paulo anali Mneneri? Ndithudi iye anali. Ndithudi iye anali. Kumbukirani usiku uja ... masomphenya apanyanja ya mafunde, ndi zina zotero? Tsopano, ndi zonse zokhudza icho. Tsopano.

Mutu wa 20 wa Woyera Wa Machitidwe, ndipo tiyeni tsopano tiyambe chapa ndime ya 27, ndipo mumvetsere mwa tcheru tsopano pamene tikuwerenga. Tsopano, uyu ndi Paulo, m'neneri, kuneneratu za chimene chidzachitike.

Pakuti Ine sindinakubisireni pakukulalikirani uphungu wonse wa Mulungu.

Munthu wodalitsikayo! O, Ine ndikufuna kudzayima pamenepo tsiku lija ndikuwona korona wa wophedwera uja atayikidwa pa mutu pake. Ngati apo pali chinthu china choti ine nditha kulira, ndiyeno ine ndidzalira, ine ndidzafuula, kumuwona Paulo.

Kumuwona Paulo Woyera, mtumwi wa mkulu uyo.

Ndi mkanjo wake utapangidwa wowala ndi wokongola.

Ndipo ine ndiri wotsimikizika uko kudzakhala kufuula pamene ife tonse tidzafika kumeneko, (Kodi inu simuli?)

87 Tsopano, "Ine sindinakubisireni kukulalikirani inu uphungu wonse wa Mulungu." Kodi uko nkulondola? Tsopano, akhristu, amayang'ana njira iyi. Ine ndikufunsani inu chinthu china chake. Kodi iye anali ndani amene anawalamulira anthu amene anali tabatizidwa mu njira ina, pambali pa Dzina la Yesu Khristu, kuti abwere ndikubatzidwa kawiri? Iye analalikirira uphungu wonse. Kodi nkulondola uko?

Ndipo nanga Paulo ananena chiyani mu ... ine ndikukhulupirira icho chinali Ine sindiri wotsimikizika, tsopano, kaya ndi Atesalonika mutu woyamba ndi ndime ya 8. "Ngati ndi ife kapena Mngelo wochokera ku mwamba akalalikira Uthenga wina wabwino...." Ngati ndi Mngelo akatsika kuchokera ku mwamba, nalalikira uthenga wina wabwino osiyana ndi uwu - wosiyana ndi kulamalira anthu kuti abatizidwe kachiwiri mu Dzina la Yesu Khristu ndipo Uthenga umenewu Paulo analalikira

Ngati Mngelo wina aliyense kuchokera kumwamba, kaya akhala bishop, kapena kadinolo, kapena oyang'anira wa onse, kapena m'busa, kapena chirichonse Ngati Mngelo atsika kuchokera ku mwamba ndipo nalikirira Uthenga wina wabwino pambali pa uwu, iye akhale wotembereredwa. Uko, nkulondola. Kodi uko nkulondola? ... Chimene Iye ananena. (Uyo ndi Agalatiya 1:8. Ine basi ndinangopezeka ndayamba kuganiza za izo. Chabwino. Agalatiya 1:8, ngati inu mukufuna kuchilemba icho, muwone chimene Paulo ananena.

88 Tsopano, Iye apa anati. Tsopano, ya 27, Ine ndikukhulupirira ndime ya 27:

Pakuti ine sindinakubisireni inu kukulalikirani inu uphungu wonse wa Mulungu. [Tsopano mvetserani chimene ichi ... mvetserani ku ulosi].

Choncho tazisamalani mwa inu nokha, ndi gulu lonse la nkhusa, pamwamba ... chimene Mzimu Woyera ... unakupangani inu oyang'anira, kuti mukadyetse Mpingo wa Mulungu, umene Iye anawugula ndi Magazi Ake a Iyeyekha.

Amene awugula ndi ndani? Amenewo anali magazi a ndani? Baibulo linanena kuti awo anali magazi a Mulungu. "Mulungu, ndi Magazi Ake a Iyeyekha." Kodi uko nkulondola? "Kudyetsa Mpingo wa Mulungu, umene Iye anawugula ndi Magazi a Yekha." Baibulo linati ife tinapulumsidwa ndi magazi a Mulungu. Kodi

inu mumachidziwa chimenecho? Ndithudi icho chimachita. Chabwino,

... anawugula ndi magazi a Iye yekha.

Pakuti Ine ndikuchidziwa ichi, kuti nditachoka ine mimbulu yolusa idzalowa pakati panu, osalekerera gululo.

Ndipo mwa inu nokha [Yang'anani, kuti munthu angayang'anane kudzera mu icho ndikuwona chinthu icho chikubwera.], kwa inu nokha amuna adzauka, kuyankhula zinthu zokhotakhota, kupatutsa ophunzira awatsate.

89 [Malo opanda chiri chonse pa tepi] ... patapita zaka ali ... kapena gulu la anthu limene limafuna kupanga bungwe, ndi kutenga opatulika ndi Mzimu Woyera kuwachotsa mu Mpingo, ndikuyikamo ma bishop, ndi mapapa, ndi ansembe ku ... iwo adzikhala oyeru,

ndi Mpingo kumakhala njira iriyonse imene iwo akufuna. Ndipo iwo adzawalipira ansembe, ndipo iye adzawapempherera iwo kuti achoke ku Gahena, ndi chinachirichonse monga chimenecho. Icho ndi chinikolayi. Mulungu anati, "Ine ndimadana nacho icho." Tsopano, mveterani. Ndiloleni ine ndiwone. Ndipo inu mukuti Mulungu ananena kuti Iye amadana nacho icho? Tsopano, tiyeni ife tiwone ngati Iye anatero:

Koma ichi iwe uli nacho, kuti iwe udana nazo ntchito za aNikolayi zimene inenso ndimadana nazo.

Mulungu amadana ndi bungwe. Uko nkulondola? Tsopano inu mukuwona ndendende chimene iwo amati achite, ndipo inu mukuwona chimene iwo anachita. Tsopano inu penyani kutsika kudzera mu Mpingo, ngati iwo sanachichite icho. Iye amadana ndi bungwe. "Iye amene ali nalo khutu muloleni iye amve chimene Mzimu akunena kwa Mpingo."

90 Tsopano, mimbulu ya Paulo inakhala aNikolayi. Iwo amayesera kukhazikitsa unsembe monga unsembe wa a Levi, umene unali chachilendo ku chiphunzitso cha Chipangano Chatsopano. Ameni. Liwu loti "Niko" liwu la chigriki "Niko" limatanthauza kugonjetsa, kupambana. Kupambana chiyani? Osonkhana, Mzimu Woyera. Kumutulutsa mu Mpingo Ambuye Yesu wowukitsidwa ndi zizindikiro ndi zozizwa pakati pa okhulupirira, ndi kuyikapo anthu amene asankhidwa mwa poponya voti kuti akhale papa, kapena Kadinolo, kapena woyang'anira. Kuyesera kuwuchotsa Mzimu Woyera kuwutalikitsa ndi osonkhana, ndi kuwupereka iwo ku dongosolo, lotchedwa dongosolo loyera la anthu, kuwayika iwo pamwamba pa osonkhana; osati kuwatchula iwo "abusa" chimene chimatanthauza "woyang'anira nkhusa," koma "bambo," chimene Yesu anati, "Inu musatchule mwamuna aliyense atate pa dziko pano." Mukuwona chinthu choyipa icho? Ndipo ife tinachitcha chiyani?

91 O, ngati ife tikanayima Ndikukhumba ife tikanati tisakhale nawo mausiku onse awa atasonkhanisidwa pamodzi motere. Ine ndikanakonda mawa usiku ndikanatenga mutu wa 12 wa Chivumbulutso, ndikukuwonetsani inu mkazi uja wakale wachigololo atakhala pamwamba apo - hule. Ndipo chifukwa chimene iye anali, chifukwa iye anali

atachita ziwerebere ... ndi Mulungu, ndipo kuzitchula iye yekha mkazi wamasiye, ndiponso iye anali mayi wa mahule. Kodi uko nkulondola?

Tsopano ife tikudziwa kuti iye anali Roma, chifukwa iye amakhala pamapiri asanu ndi awiri, ndipo chirichonse kukhala ndendende basi, ndi anthu mwa iye, ndipo iyo inali nambala ya chirombo, ndi zina zotero. Ife tonse tikudziwa izo kuchokera ku ziphunzitso zambuyomu za chomwe iye anali. koma chinthu chomvetsa chisoni cha icho, ndichakuti iye anali mayi wa mahule. Ichi chinali chiyambi chake apa - chinayamba mu Roma ngati gulu la akhristu, otchulidwa kuti akhristu.

92 Mveterani! Mulungu, mundithandize ine kuti ndichipange icho kukhala chenicheni! Gulu la akhristu mu Mpingo ngati uwo, iwo anakhala mwa mwambo ndi mosutsa, ndikutulukamo ndikuzipangira okha bungwe; ndiyeno ndikuchilumikiza icho mu M'badwo wa Mdimu ndi boma. Ndipo boma ndi Mpingo chinakhala chimodzi chiyani? Mpingo wa akhristu.

Iwo unatchedwa Mpingo wa Katolika Woyera. Liwu loti "Katolika" ndi liwu ... kutanthauza "Ponseponse," Mpingo waukulu wa Chikhristu waponseponse; ndipo kuwatchula anthu amene amayankhula mu malirime, ndi kufuula, ndi kuchiza odwala, ndi zina zotero, owukira. Ndipo mapeto ake anachipanga icho kukhala chokakamiza mpakana wina aliyense amene anapezeka akupembedza mwa njira imeneyo anagwidwa ndi kuponyeredwa mkati mwa dzenje la Mikango, ngati iwo sachifungata Chikatolika. Icho chayenda zaka mazana mazana zonsezi kumbuyo uko zachizunzo icho.

Koma Mpingo uwo sunafe. Inu simungauphe iwo. Mulungu anati iwo ukhalapo mpakana kumapeto, ndipo Iye adzaupatsa iwo korona wa moyo. Kubwera kutsika kudzera mu mibadwo iyo ya chizunzo.

93 Ndiyeno potsatira anabwera Martin Luther kudzapitiriza m'badwo, ndipo iye anaukokera Mpingo kunjira, pansa pa kulungamitsidwa.

Kodi chinachitika ndi chiyani pamene Luther anafa? Iwo anaupanga iwo bungwe, kuwupanga iwo Mpingo wa Lutherani. Iwo anapeza chiphunzitsa. Pamene iwo

anawupanga iwo bungwe, iwo anachita chiyani? Kuwupatsa iwo kubadwa kobwerera ku Chiroma kachiwiri. Ndendende kulondola.

Ndiyeno Mzimu Woyera unatulukamo mu chimenecho ndipo Wesley anachiwona icho. Ndipo Wesley ndi Whitfield, George Whitfield, ndi ena ambiri a iwo, ndi Asbury, ndi ambiri a iwo - akuluakulu azitsitsimutso - anatumikira dziko lapansi mu tsiku ilo. Iwo anali ndi chitsitsimutso mu m'badwo uwo wa Filadefiya umene unatumikira England, komanso United States.

Iwo anali ndi misonkhano kumene iwo anakankhiridwa kunja, ndipo iwo anatchulidwa oyera ozigubuduza. Inu a Methodist munachichita chimenecho. Iwo amagwa pansa, pansa pa mphamvu ya Mulungu, ndipo iwo anaponyera madzi ku nkhope zawo ndikuwakupizira iwo. Uko nkulondola. Ndipo iwo anagwedeza kwambiri pansa pa icho, mpaka iwo anene kuti iwo anali nako kugwederera. Anthu amatha kugwederera, ndi kugwedezeza pansa pa mphamvu ya Mzimu Woyera. Iyo ndi mbiri ya Chimethodist.

Kuchokera uko anabwera ogwedeza, ndi ena otero, amene

94 Tsopano iwo anachipanga icho bungwe. Iwo anachipanga Chimethodist ichi, Chimethodisti chachikale, ndipo Chimethodist cha mtundu uwu, ndipo Chimethodisti cha mtundu uwo, mpakana icho chitatsika kwambiri mpakana anthu a ChiMethodisti kufuna kuchotsamo magazi kuwatulutsa kuchokera mu mabuku awo a nyimbo.

Pano usiku wina, pa pologalamu ya pa televizion (mayi wanga anadiyitana ine) iwo anali ndi m'busa wa Methodisti konkuno ku Indiana, kuphunzitsa gwedemula mu tchalitchi. Anati, "Ndichamanyazi kuti ife talephera kuwona luso ili lokongola lomwe likulowa mu Mpingo." Uyo ndi mdierekezi, ndi m'neneri wonyenga. Kulondola. Osati kufuna kuvulaza kumverera kwanu, koma, m'bale, icho ndi choonadi cha Mulungu.

Ine ndibwino ndikukwiitseni inu pang'ono motere, ndikukupangani inu kuwerenga Lemba, mwina ndikukonza ndi Mulungu, kusiyana ndi kudzatayika kumapeto. Inu mukhoza kukhala kuti simukundikonda ine tsopano, koma tsiku lina inu mudzandikumbatira ine, ndikunena kuti, "M'bale Branham, ichi ndi choonadi." Ndi ichi

apa pompano. Iwo akulowa mu icho. Apo ndipamene iwo Icho basi chiri apo. Baibulo linati iwo adzachichita icho.

95 Ndiyeno kuchokera pa Wesley, ngati Wesley anachichita icho, ndiyeno motsatira akubwera a Pentekosite. Ndipo iwo anali ndi kubwezeretsa kwa mphatso, anayamba kuyankhula ndi malirime, ubatizo wa Mzimu Woyera. Kukhala ngati mbewu ya chimanga imene ikutuluka kuchokera mu nthaka. Chinthu choyamba, iyo imavunda; kubweretsa timasamba tiwiri. Kenako inu mudzakhala ndi munda wa chimanga, inu mukuganiza. Tsamba ilo limakula ndikupanga ngayaye. Ichi poyamba chinali chiLutherani. Ngayaye, iyo inali chiyani? Methodisti - utuchi wa mungayaye, chikondi chapa abale, ulaliki, utuchi wa mungayaye kuuluka kulowa mwa ena.

Bwanji, ngakhale chirengedwe chimalengeza za mibadwo ya Mpingo iyi. Methodisti kutuluka mu chipwirikiti ... kapena ine ndikutanthauza, Lutherani kutuluka mu chipwirikiti; Methodisti kutaya chikondi chake cha pa abale, ndi tsiku la kulalikira ndi tsiku la umishonare. Tsiku lalikulu kwambiri la umishonare limene dziko lapansi linayamba ladziwa linali munthawi ya Methodisti (Uko nkulondola), Kukutumula kuchotsa utuchi wake wamungayaye.

96 Chinachitika ndi chiyani kuchokera apo? Kuchokera mu utuchi wa mungayaye uwo kunabwera kuphatika kapeni ka chimanga, apentekosite - njere, monga ngati chinthu chomwecho kulowa mkati. Osati tsamba, osati ngayaye, koma njere. Ndipo tsopano a Pentekosite ali ndi kapuchi kukutira njere yonseyo, mpakana kuti inu simungathe kuyiwona njereyo nkomwe. Ino ndi nthawi yoti tizitsuke izo tizichotse. Amen!

Kodi iwo anachita chiyani? Anachita chinthu chomwecho chimene a Methodist anachita. Wina anawapanga iwo gulu la bungwe, anati, "Ife ndi ife a Assemblies of God"; winayo, "Ife ndife a Pentecostal Holiness"; winayo, "Ife ndife a Oneness"; "Ife ndife a Twoness." Ndipo iwo alipo ochuluka a ichi ndinso ochuluka a ichi. Kalanga ine, kukwera linunda limodzi la ngamila, malinunda awiri, malinunda atatu, zonse. O, apo pali makumi asanu ndi limodzi ... kapena, makumi atatu, kapena makumi makumi anayi mabungwe osiyana a iwo.

97 Kodi iwo anachita chiyani? Kuziponya mobweza mbuyo kulowa mu Chiroma kachiwiri, kubatiza mu ubatizo wa Mpingo wa Roma Katolika.

Ine ndinamufunsa wa Pentekosite wina aliyense kuti andiwonetse ine pamene wina aliyense mu

Baibulo anabatizidwa mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Ine ndikufunsa bishop aliyense, kadinolo, mphunzitsi aliyense, kuti andiwonetse ine pamene izo zinachitikapo, kunja kwa Mpingo wa Katolika. Ndipo Luther anazibweretsa izo pamodzi ndi iye. Iye anabweretsa katikisimu, ndi zina zonse kuchokera mu iwo. A Methodist anapitirira ndi icho.

Apentekosite, inu mukuyenera kuchita manyazi. Ziyeretseni! Bwererani ku Mawu. Lapani, kapena Mulungu adzakuchotserani choyikapo nyali, kuwala kumene inu muli nako. Amen. Chabwino.

98 Kuuchotsa Mzimu Woyera ngati mtsogoleri, ndipo muwapatse iwo dongosolo loyera la anthu, ndipo muwayike iwo pamwamba pa osonkhana. Ndipo musawatche iwo abusa, oyang'anira nkhusa (Ife tikuyenera kutchedwa abusa. Oyang'anira nkhusa, liwu loti "M'busa" limatanthauza.); koma "Atate, Kadinolo, bishop wamkulu, kapena oyanganira wamkulu."

Achoonadi eni - eni anachida chinthu ichi, ndipo Mulungu anayikira kumbuyo ichi chifukwa cha iwo, ndipo anati, "Inenso ndimadana nacho ichi," chifukwa Iye akuyenera kukhala Oyang'anira wamkulu, bishop wamkulu, papa. Iye amagwira ntchito ndi munthu payekha payekha. Osati bungwe, koma munthu.

Tsopano, mwachilendo (Mvetserani, monga pamene ife tikufika kukutseka. Ife tatsala ndi ndime imodzi.)

99 Apa ife tiri ndi chiphunzitso cha chiyambi cha Chikatolika, machitidwe wolowa m'malo a utumwi wina akachoka kapena akafa. Ndiangati omwe akudziwa zimenezo? Utumwi. Tsopano, Akatolika amati papa lero ndi olowa m'malo wa Petro - machitidwe wolowa m'malo a utumwi wina akachoka kapena akafa. Kulibeko chinthu chonga ichi.

Chiri motani chikhumbo chanu cha thupi cha kugonana ...? Zinatheka bwanji kuti Esau ndi Yakobo onse awiri anali obadwa mwa atate woyera, ndi mayi oyeri; ndipo m'modzi wa iwo mkhristu, ndipo winayo mdierekezi? Zikutheka bwanji? Chifukwa tchimo ndi tchimo, ndipo kugonana ndi kugonana; koma Mulungu amapereka kubadwa.

Mulungu anatisankha ife kuchokera ku maziko adziko lapansi. Kodi inu mumachidziwa chimenecho? Dikirani mpakana ife tifique ku kuwawerenga a zambiri yakale awa, ndipo tiwone m'mene Ireneyasi, m'mene iye akuyamikira Mulungu pomusankha iye dziko lapansi lisanakhazikitsidwe; m'mene Martin Woyera, onse a iwo, kumupatsa Iye mayamiko, kuyamika Mulungu, anati, chifukwa ... Ndipo anthu kuyankhula za iye, anati iye anasankhidwa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Ilo ndilo lemba. Abale amene aja amayima mu mzere ndi Mulungu.

Koma Mpingo wachikale wakuda uwu unabwera kudzera mu zaka mazana khumi ndi asanu za Mbadwo ya Mdimba izo, amafafaniza chinthu chonsecho monga ngati nyali ikutulutsa utsi, kukupangitsa khungu kuwala. Koma padzakhala kuwala mu nthawi yakumadzulo, Ambuye anatero.

100 Kulowa m'malo kwa utumwi pambuyo pa wina, papa m'modzi ... ndipo iwe uyenera kukhala mu m'ndandanda iwe usanakhale papa. O, kalanga, kalanga ine! Izo ndi zamkutu. Osonkhana ... osati oyeri ndi olungama, koma aloleni ansembe awapempherere iwo, ndipo awatulutse iwo mumachimo awo, kuwakhululukira machimo awo, kupereka ndalama pa kuvomereza.

Achiprotestant amachita chimodzimodzi. Iwo amayetsera kumusisita m'busa wawo pa msana, ndikumakhala monga ena onse a mu dziko lapansi. Ndipo iye, samadziwanso zambiri zokhudza Mulungu kuposera momwe iye amadziwira, kuwalola iwo kukhala mu Mpingo mwake, ndikumawatchula iwo mamembala a Mpingo wake; ndikuwalola iwo kumakhalabe m'menemo, ndikumanenera kwa iwo kuti iwo apulumutsidwa. Iwo adzakhala okhumudwa motani pa tsiku ilo, ngati iwo sanabadwensu mwatsopano! Popanda Mzimu Woyera, inu mwayatika. Palibe munthu amene anganene kuti Yesu ndi Khristu, koma ndi Mzimu Woyera wokha basi.

101 Mpingo woona waku Efeso sunanyengedwe ndi zoyankhula zopukutidwa, ndi zaluntha izi. Iwo anadana nacho icho. Iwo sananyengedwe. Iwo akudziwa Mpingo woona sunatero. Vumbulutso lonyenga, limene amuna awa anali nalo, lotchedwa Chinikolayi, limene sirimagwirizana ndi Mawu a Mulungu.

Mundiwuze ine pamene inu munaona mu Baibulo akuphunzitsa za wansembe akulapitsa machimo. Ndipati pamene inu munawonapo kukonkha kukuphunzitsidwa mu Baibulo pano kuchikhululukiro cha machimo? Ndipati pamene inu munawonapo wina wake akubatizidwa mu Dzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera kuchikhululukiro cha machimo awo? Ndipati pamene inu munawonapo chiyanjano chogwirana dzanja la manja, ndikulemba maina awo mu buku la Mpingo mkati umu? Ndipati pamene inu munayamba mwaonapo zinthu zonsezi?

Kodi ichi ndi chiyani? uwu ndi unsembe, kapena utsogoleni wa mpingo, umene suli wolondola ndi Mawu, ndipo awa ndi aNikolayi. Ndipo Mulungu anati, "Ine ndimadana nawo." Bwererani ku Mawu. O, Ine ndikudziwa icho ndi cholimba, abale, koma Ine sindikutenga gawo. Zikanganani ndi Iye.

102 Vumbulutso lonyenga, losakhala ndi Mawu, koma anawatcha iwo onama, atumwi onyenga, aneneri onyenga.

Koma Mpingo woona unagwiritsabe chiphunzitso cha pachiyambi cha Paulo Woyera, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera ndi zizindikiro zikutsatirapo, ndikutsimikizira Mawu amene Paulo anaphunzitsa. Amen! Mundiwonetse ine pamene Mulungu adzatsimikizire Mawu a kukonkha. Mundiwonetse ine pamene Mulungu adzatsimikizire ndi kubweretsa kuyankhula ndi malilime, ndi zinthu zazikulu, basi pongogwirana chanza ndi abusa pena pake, ndi kulemba dzina lanu m'bukhu; ndi kukhala mudakatafunabe, kusuta, kumwa, kunena mabodza, maphwando amakadi, kukhala nacho chisangalalo pang'ono, kupita O, chifundo! Izo ndi zachithupithupi, aneneri onyenga, abwenzi. Inde, bwana.

103 Njira ya Mulungu ndi chiyero. Mulole ichi chidziwike kwa membala aliyense pano wa thupi la Khristu; mpakana inu mutakhala moyo wachiyero, Mulungu amakana nsembe yanu. Nsembe ikuyenera kuperekedwa ndi manja oyera. Uko nkulondola. Wansembe

wamkulu, iye asanalowe mkati kudzapereka nsembe, iye amayenera kukhala woyera, ndipo wodzipereka ndi wodzozedwa, ndipo wonunkhira, ndi china chirichonse, iye asanalowe ndikuyenda pamaso pa Mulungu kuti adzapereke nsembe. Kodi uko nkulondola? Ndiyeno inu mungatuluke bwanji kunja uko ndikukanama, ndikukaba, ndikukachita mkangano, ndi kukachita ndewu ndi oyandikana nawo nyumba ndi china chirichonsecho, ndikupitiriza momwe inu mukuchitira; ndiye kenako inu ndikulowa mkati ndikunena kuti, "O Ambuye Mulungu! Yesu alemekezeke! Aleluya!"

Anthu amati, "Ine ndinawona iwo akuyankhula mu malirime." Ichobe sichikutanthauza kuti iwo alinawo Mzimu Woyera. "Ine ndinawamva iwo akufuula." Ichobe sichikutanthauza kuti iwo alinawo Mzimu Woyera. Mzimu Woyera ndi moyo.

104 Baibulo linati, "Mvula imabwera pa dziko pafupipafupi, kulikonzekeketsa ilo, kulikonza ilo, kuchimene ilo lakonzekedwetsera [Ahebr 6], koma minga ndi nthula zimene zikuyandikira ku kukanidwa, zimene chimaliziro chawo ndi kuwotchedwa."

Dzuwa limawalira pa olungama ndi osalungama yemwe. Mvula imagwa pa olungama ndi osalungama omwe. Mvula imabwera kudzaipanga mbewu ya tirigu, ife tiyitchula iyo, ndi udzu wonse umene uli m'munda. Ngati tirigu ali ndi ludzu, koteronso udzu uli ndi ludzu. Ndipo mvula yomweyo imene imathirira tirigu, yomweyo imathiriranso udzu.

Tirigu wamng'ono wakale uyo adzayimika mutu wake ndikufuula, "Ambuye alememkezeke! Aleluya! Aleluya! Ine ndiri wokondwa poyipeza mvula iyi."

Udzu waung'ono wakale iwonso udzafuula, "Ulemerero kwa Mulungu! Mulungu alememkezeke! Aleluya! Ine ndiri wokondwa poyipeza iyo."

"Koma ndi zipatso zawo inu mudzawazindikira." Uko nkulondola. "Ndi zipatso zawo inu mudzawazindikira iwo."

105 Ndime ya 7, ndipo kenako ife tikutseka. Ichi ndi chotsirizira cha m'badwo wa Mpingo. Tsopano, ife titchedwa ndi pafupi mphindi zisanu, kapena khumi, basi kamphindi.

Iye amene ali nalo khutu, muloleni Iye amve chimene Mzimu anena kwa mipingo; kwa Iye amene alakika Ine ndidzamupatsa iye kuti adyeko za kumtengo wa moyo, umene uli pakati pa paradizo wa Mulungu.

Tsopano tawonani, abwenzi, pano pali njira ya m'mene inu mungagonjetsere. Choyamba inu mukuyenera kugonjetsa, kenako inu mukhoza kudya chipatso. Ndi m'gonjetsi. Inu mukukumbukira usiku wina, phunziro lathu usiku watha? Yohane amayenera kulowa mu Mzimu Iye asanawone chirichonse.

Ndipo zingatheke bwanji inu kukhala apo, ndi kumanena, "Ngati iye sali wa Baptist, ine sindimumvetsera Iye?"

"Ngati iye siali wa Chipresbateri, ine sindimumvetsera Iye."

"Ngati iye sangaphunzitse basi ndendende chimene Mpingo wanga umaphunzitsa, ine"

Inu simungagonjetse. Inu simunalowe mu Mzimu apobe. Inu muli kunja kwa dongosolo. Lowani mu Mzimu. Nenani, "Ambuye Yesu, ine ndimakukondani inu. Tsopano muwulule kwa ine chirichonse chimene Inu mukuchiwona kuyenera. Basi mungochibweretsa icho kwa ine." Ndiyeno inu mupeze zonse zolondola. Uko nkulondola.

106 Zindikirani, maulendo atatu Baibulo lakhala likuyankhula za Mtengo wa Moyo mu Genesis, maulendo atatu mu buku la Chivumbulutso. Tsiku lina ife tinachiyankhula chimenecho. Mukukumbukira? Lamulungu, dzulo

Mdierekezi amadana ndi chidutswa cha Lemba chimene chiripo pamenepo. Koma Iye amadana kwambiri ndi Genesis ndi Chivumbulutso. Iye amaukira Genesis chifukwa ... kutsimikiziridwa kwa ilo, chifukwa iye amafuna kuwapanga anthu kukhulupirira kuti sizinali chomwecho - Genesis sanabwere mu njira imene Mulungu ananena kuti iwo anabwerera, kuti china chake chapadera chinapangitsa chirengedwe ichi ndi zinthu. Iye amaliukira ilo mu njira imeneyo. Ndipo iye amawachotsa anthu kuwatalikiritsa ndi Chivumbulutso chifukwa ilo limamuvumbulutsa Yesu monga kukhala Mulungu, ndi iye kukhala m'dierekezi. Ndipo iye wathedwa. Ndipo ulemerero wa Mpingo woyetsedwa

ukupita kwawo kwa Mulungu, ndi kuthedwa kwa m'neneri wonyenga, ndi onse onama ndi kuchita chirichonse, adzaponyedwa mu Nyanja ya moto - ndizosadabwitsa kuti iye akuwatalikiritsa iwo kwa ilo.

Koma kumbukirani, malo onse awiri akukamba za Mtengo wa Moyo umene uli mu paradizo.

107 Tsopano, tiyeni ife titenge ichi kwa mphindi chabe. Ndipo tsopano mtengo. Yohane Woyera, mutu wa 6, ngati inu mukufuna kuti muzilembe izo, Yesu anati, "Ine ndine mkate wa moyo." Tsopano kumbukirani ... tsopano, ife tigwiritsa tchito nsanamira ziwiri izi ngati choimira pano, kotero ... basi tisanatseke tsopano.

Tsopano, ku dzanja langa lamanja ndi mtengo m'munda wotchedwa "Mtengo wa Moyo." Kudzanja langa la manzere ndi mtengo m'munda umene ukutchedwa "mtengo wa chidziwitso." Ndiangati amene akudziwa kuti Baibulo likunena kuti uwo unali Mtengo wa Moyo ndi mtengo wa chidziwitso? Tsopano, munthu amayenera kukhala moyo ndi Mtengo uwo wa Moyo; osati kugwira mtengo wa chidziwitso. Kodi uko nkulondola?

Ndipo kwa nthawi yoyamba pamene iye anawukhuza iwo, iye anazilekanitsa yekha kuchokera kwa mulengi wake. Iye anataya chiyanjano chake ndi Mulungu pamene iye anatenga kuluma kwake koyamba kwa chidziwitso. Tsopano, ganizani molimba tsopano. Ndipo inu amene mukulemba zolemba zanu, ine ndikupatsani inu nthawi, kotero kuti inu muchimve ichi, chifukwa ine sindikufuna kuti inu muchiphonye ichi.

108 Yesu, mu Yohane Woyera 6, iwo amamwa kuchokera kukasupe, ndi kukweza manja awo ndi kuyamba kunyoza apo; kuti makolo awo anamwa ku chokera mu thanthwe la Uzimu ndi zotero. Iye anati, "Ine ndine Thanthwelo limene linali mu chipululu."

Ndipo iwo anati, "Pano inu mukunena kuti inu munali mulipo Abrahamu asanakhalepo, ndipo inu ndi munthu amene zaka zanu sizinadutse makumi asanu. Ndipo inu mukuti munamuona Abraham? Ife tsopano tikudziwa kuti ndinu wamisala. Inu ndi mdierekezi," mwaona?

Iye anati, "Abrahamu asanakhalepo. INE NDIRI." INE NDIRI anali pa chitsamba ndi Mose, chitsamba choyaka moto. INE NDIRI. "Abrahamu asanakhalepo, INE NDIRI" - osati "Ine ndinali". Tsopano, inu anthu amene mumanena kuti masiku azozizwitsa anapita, inu mukuyenera kulipanga Lemba limenelo kumanena kuti, "Ine ndinali wamkulu amene ndinali." Mwaona. Osati "Ine ndinali," kapena "Ine ndidzakhala," "INE NDIRI." Icho ndi nthawizonse. Iye ndi wamuyaya. Mawu oti INE NDIRI ndi amuyaya: m'badwo wathu wonse, nthawizonse, mu zoyikapo nyali zonse zisanu ndi ziwiri za Golide, Mpingo uli wonse, malo aliwonse, mtima uli wonse. INE NDIRI. Osati "Ine ndinali," kapena "Ine ndidzakhala." "Ine ndine tsopano monga chimene Ine ndinali nthawi zonse," mwaona. Nthawi zonse, INE NDIRI.

109 Iwo anati, "Makolo athu Ife sitikukudziwani inu Ife tazindikira inu ndinu mdierekazi." Anati, "Makolo athu anadya mana mu chipululu kwa nthawi ya zaka makumi anayi."

Ndipo Yesu anati, "Ndipo iwo onse anafa." Uko nkulondola? "Iwo onse anafa. Koma Ine [O!] Ine ndine mkate wamoyo umene uchokera kwa Mulungu kuchokera kumwamba. [Mkate wa moyo.] Ngati munthu adya mkate uwo iye sadzafa."

"Kodi munthu uyu adzapereka thupi lake kuti lidyedwe?" Iwo anatero. "Tsopano, Iyeyu ndi wamisala, ntheradi."

Mkate wa Moyo umachokera mu Mtengo wa Moyo, kumene iwo amadya kuchokera m'munda wa Edeni. Iye anali Mtengo wa Moyo. Tsopano ngati Mtengo wa Moyo anali munthu, ndiyeno mtengo wa chidziwitso unalinso munthu. Tsopano inu mukuti serpent analibe mbewu. Ngati moyo umabwera kudzera mwa mwamuna, imfa imabwera kudzera mwa mkazi. Chabwino. Mkaziyo anali mtengo wa imfa.

110 Nthawi yomweyo uyu atamuyipitsa iye - chimene iye anachichita, serepenti - iye anati, "Serepenti anandinyenga ine." Uko nkulondola. Osati njoka. Iye anali wochenjera kwambiri pa nyama zonse. Iye anali pakatikati pa chimpanzi ndi munthu. Mbewu ya nyama singathe kulowana ndi mkazi - iyo singathe kutero. Koma mwamuna uyu anali Iye anali chirumikizo choyandikana ndi icho. Ndipo Mulungu anayika themberero la

mtundu umenewo pa iye, Iye amamuyika iye kumubwezera ku mimba yake, wopanda miyendo; ndipo

anachotsa fupa lina lirilonse mwa iye ndikulisintha ilo kuchokera ku chirichonse chokhala ngati munthu. Sayansi kuyesera kuchikumba icho mudothi.

Icho chabisika mu zinsinsi za Mulungu, pakati pa paradizo wa Mulungu. Apo pali vumbulutso lanu.

111 Iye anabereka mwana wache woyamba amene anali Kayini (Kodi uko nkulondola?), mwana wa satana. Mwana wa satana. Ngati iye sanali, nanga choyipa chija chinachokera kuti? Kuchokera kwa Adamu, amene anali mwana wa Mulungu? Chinachokera kwa mdierekezi, atate wake. Ndipo iye anapha - wakupha woyamba anali m'dierekezi, mwana wa m'dierekezi. Tawonani chimene chinachitika. Zitatha izo, wonani mzere wa mibadwo ya Kayini.

Pansi kudzera mu m'badwo uwo umene unatsatira pambuyo pa Kayini onse anali asayansi ndi zimphona. Werengani Baibulo. Iwo anamanga nyumba, iwo anagwira ntchito ndi chitsulo, ndipo iwo anali asayansi. Koma wina aliyense amene anachokera kwa Seti (amene ... Abele atafa - kufaniziridwa ndi Yesu, anafa. Ndipo Abele anafa, ndipo Seti anatenga malo ake. Kufa, kuyikidwa, ndikuwuka kwa akufa.), kuchokera kwa iye kunabwera alimi odzichepetsa, oweta nkhusa anachokera kumeneko.

112 Tsopano Yesu anati, "Makolo anu anadya mana mu chipululu ndipo iwo onse anafa. Koma Ine ndine mkate uwo wa Moyo." Mkaté wanji wamoyo? Kuchokera ku Edene, "Umene munthu akadye mkate uwo ndipo sadzafa."

Tsopano, Mulungu anayika M'ngelo kuzungulira Mtengo wa Moyo uwo kuwulondera iwo, kuti wina aliyense asaukhuze iwo, pokhapokha ngati iwo akanadya Mtengo uwo ndikukhala ndi moyo kwa muyaya. Kodi uko nkulondola? Chifukwa iwo akanatha kupitiriza ndi mtengo uwo ndi kufa. Kodi uko nkulondola? Chifukwaponse pamene iwo amadya za mtengowo amafa. Ndipo basi motsimikiza monga inu mungafé chifukwa chokudya zochokera mu mtengo wa chidziwitso....

Tsopano tiyeni ife tiyang'ane ku mtengo wachidziwitso tsopano. Tiwone chimene iwo wachita. Tsopano tiyeni tiwone chimene iwo wachita. Chinthu choyamba, tiyeni ife tichiwone icho Chabwino, tiyeni tiwone chimodzi chomwe iwo Icho chinapanga onga wa mfuti. Iwo ukupha abwezi athu. Uko nkulondola, kuphana wina ndi mnzake ndi onga wa mfuti, wochokera ku mtengo wa chidziwitso. Chotsatira chimene tachita, bwanji, tiyeni tione. Ife tinapanga galimoto kuchekera ku mtengo wa chidziwitso umenewo. Iyo ikupha ochuluka kuposa momwe onga wa mfuti ukuchitira. O, inde. Tsopano ife tiri ndi bomba la haidrojéni.

Mulungu samawononga kanthu. Munthu amaziwononga yekha ndi chidziwitso chake.

113 Koma zonsezo ndi zakwa Mulungu, Mulungu adzachidzutsanso icho kachiwiri. Mulungu samaluzá kanthu. Yesu ananena choncho. Uko nkulondola. "Iye amene adya mkate uwo ali nawo moyo wosatha, ndipo ine ndidzamudzutsa iye pa tsiku lomaliza." Ilo ndilo lonjezo Lake. Tsopano, Mulungu Iwo anapitiriza, kudya pa mtengo wa chidziwitso ndi kumafa. Koma mofulumira pamene iwo akanafika ku mtengo uwo, iwo akanakhala moyo kwa muyaya.

Kotero tsopano, m'malo moti M'ngelo kunjá uko kuwaletsa kuti asauyandikire mtengo uwo, iye ali kunjá uko kuwawongolera iwo mozungulira ku mtengo uwo - Angelo a Mipingo, Mipingo isanu ndi iwiri, kuwabweretsa iwo ku Dzina la Yesu Khristu, amene ndi Mtengo wa Moyo umene wayima mu paradizo wa Mulungu. Psyfuu! Kalanga ine! Ine ndikuyembekezera kuti inu mukuchimvetsa icho - Mtengo wa Moyo wukuyima mu paradizo wa Mulungu, kuti inu mukadyeko pa Iye ndi kukhala mwana wa mwamuna ndi mwana wa mkazi wa Mulungu, ndikukhala ndi moyo kwa muyaya. "Iye amene amva Mawu Anga ndikukhulupirira pa Iye amene anandituma ine ali nawo moyo wamuyaya, ndipo sadzabwera mu kuweruza, koma wachokera ku imfa ndikulowa m'moyo.

114 M'bale, mulongo, tsopano ine ndikutsimikiza ine ndakudaulirani inu, kukuvulazani inu. Ine sindimatanthauza kuchichita icho mu njira imeneyo, mwaona? Mulungu akudziwa chimenecho. Koma ine ndikuyenera kuchichita icho mwa njira imeneyi kuti tikuloleni inu

kuwona pamene ife tiri. Ine sindikukhulupirira kuti ife tiri ndi nthawi yochuluka yokhala. Ine sindikuyesera kukuchotsani inu pa Chikhristu chifukwa inu ndinu a bungwe. Icho sichimenecho. Anthu ndi amene ali ovulála a zochitika. Iwo sakudziwa choti achite. Chonse chomwe makolo awo achita nthawi zonse ndi kupita ndikukajowina tchalichi ndi zinthu. Koma, m'bale, chinthu chimodzi ife tisanachoke, ndiloleni ine nditengepo chowerenga chimodzi. Mneneri anati Kodi inu mumawakhulupirira aneneri? Baibulo limanena kuti tidziwamvera iwo. Mneneri anati ikubwera nthawi imene sipadzakhala usana kapena usiku, koma lidzakhala ngati tsiku la chimbuuzi. Koma munthawi ya kumadzulo, basi dzuwa lisanalowe, padzakhala kuwala. Kodi uko nkulondola?

115 Tsopano, onani chimene ife takhala nacho. Tsopano tiyeni basi tingoyang'ana. Kodi ichi chima.... Kodi dzuwa limatuluka kuti, mwa chilengedwe? Ku m'mawa. Kodi uko nkulondola? Ilo limalowa ku madzulo. Ine ndikanakonda ndikanakhala.... Ine ndidzawatenga mapu m'mawa usiku ndikukuwonetsani inu.

Pamene Mzimu Woyera unagwa mu Yerusalemu, iwo umapanga nambala yangwiro ya 8, momwe umadutsa. Iwo umapita molunjika chopingasa kulowa mu Ireland, kubwerera kuzungulira, pamwamba, ndikubwerera ku gombe la kumadzulo, ndikugwa mobwerera kachiwiri - nambala yangwiro 8, kumene Uthenga unapita.

Tsopano chitukuko chakhala chikuyenda ndi dzuwa. Ndiangati amene akudziwa chimenecho? Inu munaphunzitsidwa chimencho, ndipo mukudziwa icho. Chitukuko chakale chimene ife tiri nacho ndi China. Ndipo kotero kuchokera apo, iye wabwera mopingatsa chakum'mawa. Ndipo pamene Mzimu Woyera - osati S - U - N, koma S - O - N

116 Pamene dzuwa, wa S - U - N -, lidzayamba kuwala kutsika kudzera mu chifunga, ndi nkhangungu ya usiku, ziribe kanthu kaya mbewu iri kuti, iyo idzakhala ndi moyo, chifukwa moyo wa zomera zonse umakhala moyo ndi dzuwa. Ife tikudziwa zimenezo. Inu mukhoza kukhuthulira konkire kudutsa chidutswa cha udzu, ndipo nyengo yophukira, kodi udzu wokhuthala uli kuti? Kumapeto peto kwa konkire. Chifukwa chiyani? Ndi moyo uja. Pansi apo inu simungabise moyo weniweni. Moyo waung'ono uwo, mofulumira pamene iwo

uzindikira kuti dzuwa likudutsa pamenepo, iko kadzakwawa mu njira yake kwa mtunda wautali kudutsa nyumba zingapo za mumzinda, kudutsa mozungulira pansi pa konkire uyo mpakana katatulutsa mutu wake pa mwamba, ndikuyamba kupembeza Mulungu. Inu simungabise moyo. Uko nkulondola, moyo.

Pamene inu mwabadwa mwatsopano inu simungachibise icho. China chake chikuyenera kulira mokweza pamene inu mwapeza moyo.

117 Tsopano, zinthu zonse zimene ndizakufa tsopano, ndipo mbewu zazing'ono zathetheka, zamkati zimatulukamo ndipo iyo imafa. Koma moyo umakhala uli momwemo. Tsopano, pamene dzuwa liyamba kuwala mu nyengo yophukira, maluwa ang'ono adzatuluka, ndipo chirichonse chitulutsa mutu wake m'mwamba kachiwiri kutuluka kuchokera pansi pa zidutswa, kutuluka kuchokera pansi pa zipika, kutuluka kuchokera pansi pa matanthwe. Iyo idzakulanso kachiwiri, ndikukhala moyonso kachiwiri (Kodi uko nkulondola?) Chifukwa dzuwa s-u-n likuwala.

Tsopano, tsiku lina S - O - N adzawala, amene ndi woyambitsa wa moyo wamuyaya, ndi china chirichonse chimene chameretsedwa kwa Iye ku moyo wamuyaya, Iye anati, "Ine ndidzaukitsa iwo mu masiku otsiriza." Inu mukuwona chimene ine ndikutanthauza? Moyo wamuyaya udzadzutsidwanso mu masiku otsiriza.

Ngati iwo angakukwirireni inu mu Nyanja, iwo kulitentha thupi lanu ndi ndikulimwazira ilo ku mphepo zonse zinayi za dziko, Mulungu adzalidzutsa ilo mu masiku otsiriza. Ngati inu munakhutitsa mimba ya mkango wanjala, kapena kulowa mu maenje a lawilawi amene adzatenge Mafuta onse khumi, asanu ndi limodzi oyaka, ndi kuwala kwakukulu, ndi chiri chonse kuchokera mwa inu, Mulungu adzachidzutsa icho. "Tsitsi lomwe lapamutu panu ndi lowerengedwa." Amen. Mulungu adzalidzutsa ilo.

Tsopano, yang'anani kuno. Tsopano ngati munthu ali yense amwalira chifukwa cha mkazi, kotero munthu aliyense akhala ndi moyo chifukwa cha mwamuna. Kutengapo gawo la mkazi mu moyo wa mtundu umenewo, inu mukudziwa inu mudzafa. Palibenso njira yotulukira pa icho, inu mufa basi. Ndipo motsimikizira ngati inu mungatenge gawo la icho inu mukhala ndi moyo. Palibepo njira yotulukira icho, inu muyenera kukhala moyo.

Ameni. Ngati icho chingabereke imfa yeniyeni, ichi chibereka moyo weniweni. Iyo ndi njira yokhayo imene inu mungalandirire icho, ndikukhala ndi moyo.

118 Tsopano, Mneneri anati, padzakhala kuwala mu nthawi ya kumadzulo. Tsopano tawonani. Iye anati apo padzakhala tsiku limene lidzakhale lachimbuuzi. Ilo silidzatchedwa masana kapena usiku. Ilo ndi lokhala ngati lamitambo, lachifunga, tsiku lozizira; koma dzuwa likupereka kuwala apobe. Kutali, pamwamba pa zifunga ndi mitambo, ndi zina zotero, dzuwa likupereka kuwala kwake. Ilo likupereka kuwala kokwanira koti inu mutha kuyenda, ndipo inu mutha kuwona momwe inu mungayendere, ndi zina zotero. Komabe, ilo si tsiku lowala bwinobwino, mwaona.

Tsopano, palibe chiri chonse, chimene chingathe kukhala moyo mu tsiku ilo. Ngati inu mungadzale chirichonse pansi pa china chake pamene dzuwa silikumachiombera icho, icho chimapinimbira. Kodi uko sikulondola? Inu alimi mukuzidziwa zimezo. Kudzala chimanga munthunzi, kapena pena pake, bwanji, icho chimapinimbiritisa icho. Fred, inu mukuyenera kuzidziwa izo ndi tirigu wanu. Inu kumubzala kunja uko, ndipo ngati inu mukhala ndi nyengo ya chirimwe yoyipa, O, yozizira ndi yamvula, iyo imamupinimbiritisa iye.

119 Chabwino, ilo ndilimene liri vuto ndi Mpingo. Kudutsa kupyola m'mibadwo yonse, iwo wapinimbiritidwa. Iwo wapinimbiritidwa ndi zipembezo - lembani dzina lanu mu bukhu. Ife tinali nako kuwala kokwanira kuti tidziwe kuti apo pali Mulungu. Ine ndi wokondwa ku icho. Ife tinali nako kuwala kokwanira kuti tidziwe kuti apo pali Khristu, pali chiweruziro chomwe chikubwera. Ife takhala tiri nako

kuwala, kotero ife taika maina athu mu mabuku, ife tinagwirana chanza ndi abusa, ndi zina zotero, ndikuchita izo. Chabwino. Koma tsopano ndi nthawi ya madzulo. Tsopano, chitukuko chinabwera kuchokera ku m'mawa kufika kumadzulo, ndipo tsopano ife tiri pa gombe la kumadzulo. Ife sitingathe kupitirira apo. Ife tikaoloka, tabwereranso kum'mawa kawiri. Ife sitingapite mopitirira apo. Ife tiri pa gombe la kumadzulo.

Koma tsopano ndi nthawi ya kumadzulo. Tsopano, chitukuko chikubwera kuchokera ku m'mawa kulowera ku madzulo. Ndipo tsopano ife tiri pagombe

lakumadzulo. Ife sitingapite patali. Ife sitingapite patali. Ife tawoloka, ife tabwerera ku m'mawa kachiwiri. Ife sitingapite patali. Ife tiri pa Gombe la kum'mawa.

120 Tsopano Baibulo linati, "Nthawi ya kumadzulo kuwala kudzabwera." Tsopano, ndi dzuwa la mtundu wanji limene limawomba mu nthawi ya kumadzulo? Kodi iri ndilosiyana ndi dzuwa limene limatuluka ku m'mawa? Ndi dzuwa lomwelo. Kodi uku nkulondola?

Chabwino, kenako, ndi chiyani chimene Mulungu analonjeza? Tsopano ife tikupita kukachipeza ichi, chigwiritseni icho pano mu m'badwo uno. Baibulo linatero. Ine ndichitsimikizira icho mu mibadwo ya Mpingo iyi pamene ife tikupitiriza, kuti mu nthawi ya kumadzulo kudzatumphuka kuwala madzulo, kumene kudzabweretsenso Dzuwa la chilungamo kachiwiri, ndi machiritso m'mapiko mwake.

Ndipo zizindikiro zomwezo, ndi zodabwitsa zomwezo zimene zinachitika mbuyo uku ku m'mawa, zizachitikanso apa kumadzulo, ndi kutsanulidwa kwinanso kwa Mzimu Woyera mu masiku otsiriza.

Padzakhala kuwala munthawi ya kumadzulo,

Njira yaku ulemerero inu ndithudi mudzayipeza;

Umo mu njira ya madzi, uko ndi kuwala lero,

Kukwiridwa mu Dzina lodabwitsa la Yesu.

Ang'ono ndi akale, lapani kumachimo anu onse,

Mzimu Woyera ndithudi udzalowa Mkati;

Nyali za madzulo zabwera.

Ichi ndi choonadi kuti Mulungu ndi Khristu ndi m'modzi.

O, padzakhala kuwala mu nthawi ya kumadzulo,

Njira yaku ulemerero inu ndithudi mudzaipeza;

Mu njira iyi ya madzi ndi kuwala lero.

Kukwiridwa mu Dzina lodabwitsa la Yesu.

Ang'ono ndi akale, lapani ku machimo anu onse.

Mzimu Woyera ndithudi udzalowa mkati;

Kuwala uko kwa nthawi ya madzulo kwafika

Chinthu chomwecho chimene Petulo ananena, "Lolani ichi chidziwike kwa inu, kuti Mulungu wamupanga Yesu yemweyo, amene inu munamupachika, zonse Ambuye ndi Khristu. Lapani ali yense wa inu," iye anati, "ndipo batizidwani mu Dzina la Yesu Khristu kuloza kuchikhululukiro cha machimo anu."

121 Ndiloleni ine ndikuwuzeni kanthu kena. Monga ine ndinayankhula tsiku lina pa zakamwedwe ka mankhwala ka dokotala, anthu samakonda kutenga ndondomeko yakamwedwe kamankhwala ka dokotala. Ngati iye ali ndi njira imene ingachize matenda anu, ndipo inu mukukana kuyitenga iyo, ilo silikhala vuto la dokotala kuti inu mwafa. Ayi, bwana. Ilo ndi vuto lanu, chifukwa inu munakana kuyitenga iyo.

Ndipo tsopano, ngati dokotala alemba ndondomeko ya kamwedwe ka mankhwala ndipo inu ndikutenga ndondomeko imeneyo kupita nayo kwa venda wa mankhwala, ndipo iye ndikuyikamo chinachake m'menemo chimene sichimayenera kupezeka m'menemo, chimenecho chidzakuphaninso inu; kodi uko nkulondola? Dokotala anachiphunzira chimenecho mpakana iye akudziwa kuti muli chiphe chochuluka mu ndondomeko iyo chimene chingaphe tizirombo timene tiri mu thupi lanu. Ndipo muli zotetezera zokwanira m'menemo zimene zingatembenuze chiphe kuti icho chilephere kukuphani inu. Ndipo icho chikuyenera kukhala pa mulingo wake. Ngati inu muthiramo zotetezera zochuluka, izo sizingamuthandize wodwala; kuthiramo chiphe chochuluka, icho chingomupha iye. Icho chikuyenera kukhala pakatikati.

122 Funso linali loti, "Kodi mulibe mvunguti mu Giliyadi? Kodi kulibe sing'anga kumeneko?" Anatero m'neneri. "Nanga ndi chifukwa chiyani nthenda ya mwana wanga wamkazi sikuchiritsidwa?" Pali vuto lanji kuti ife tiri ndi Mpingo yochulukwa yakale yodwala? Chifukwa tiri ndi mavenda ogulitsa mankhwala amene akupereka ndondomeko ya kamwedwe ka mankhwala kolakwika. Uko nkulondola.

Iye sananenepo kuti, "Atate, Mwana, Mzimu Woyera." Kodi ndondomeko ya kamwedwe ka mankhwala inati bwanji? Pano pali Petulo. Ndi angati amene akudziwa kuti iye anali ndi mafungulo amu ufumu? Yesu ananena choncho. Kodi Iye ananena kuti

chiyani? Mu mawu ena, iye ali ndi cholemba cha ndondomeko ya kamwedwe ka mankhwala.

Pamene iwo anamva ichi onse anapanga phokoso iwo amakuwa, kufuula, kulankhula mu malirime ndi kukhala nayo nthawi ya mtundu umenewo. Ndipo iwo anati, "Anthu awa akhuta vinyo watsopano."

Petulo anati, "Anthu awa sanaledzere naye vinyo watsopano, monga momwe inu mukuganizira, wonani ili ndi ora lachitatu la tsiku. Koma ichi ndi chija chimene chinanenedwa ndi Mneneri Yoweli, 'Chidzachitika mu masiku otsiriza, atero Mulungu, Ine ndidzathira cha Mzimu Wanga pa thupi lililonse. Ana anu amuna ndi ana anu akazi adzanenera, ndipo pa azakazi anga ndi pa antchito anga ndidzathira cha Mzimu wanga, ndipo iwo adzanenera.'"

"Ndipo Ine ndidzawonetsa zizindikiro m'mwamba, ndi padziko la pansu, moto, ndi utsi, ndi munthunzi. Ndipo zidzachitika kuti wina aliyense amene adzayitanira pa dzina la Ambuye adzapulumuka."

123 Ndipo chinanso iye ananena zokhudza Davide: Iye anati, "Kholo lathu Davide anachiwoneratu icho, ndipo iye anati, 'Kuwonjezera apo thupi langa lidzapuma mu chiyembekezo; chifukwa Iye sadzasiya moyo wanga mu Gehena, kapena kuti sadzalola Oyera Wake kuti awone chivundi.'"

Ndiloleni ine ndiyankhule kwa inu mwaufulu, abale, za kholo lathu Davide. Iye anafa komanso kuyikidwa m'manda, ndipo manda ake ali ndi ife mpaka lero lino. [Mwaona?] Koma iye, pokhala m'neneri, anawona chiukitsiro cha Khristu ... Lolani ichi chidziwike kwa inu, kuti Yesu uyu, amene inu munamupachika ndi manja anu oyipa, Mulungu wamupanga Iye zonse ziwiri Ambuye ndi Khristu."

Pamene iwo anamva ichi, iwo analaswa mumitima yawo, ndipo anati, "Amuna inu abale," Kapena "Dr. Simoni Petulo, tirembereni ife ndondomeko ya kamwedwe kamankhwala. Kodi ife tingachipeze bwanji ichi? Iye tikufuna chimene chingachize tchimo lathu." O.

124 Tsopano tamuwonani iye, chimene iye ananena. Tsopano inu mupapeza pamene Mpingo iyi inachoka pa mzere. Iye anati, "Dikirani mphindi. Ine ndikulemberani inu ndondomeko ya kamwedwe ka mankhwala, ndipo iyo ikhala ndondomeko ya muyaya. Iyo ikhala ya inu, ndi ya ana anu, ndi kwa iwo amene ali kutali, ndipo ngakhale ochulukwa monga Ambuye Mulungu wathu ati adzawayitane."

Kodi iye ananena chiyani? kodi iye anachikonza bwanji icho? Monga momwe Katolika aliri nacho icho? Monga momwe a Baptist aliri nacho? Monga momwe a Methodist aliri nacho icho? Aliyense wa iwo wawonjezera china chake kapena kuchotsera china chake kuchokera pa icho. Monga a Pentekosite? Iwo anawonjezera kapena kuchotsera. Koma iye anayankhula chiyani? "Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza kuchikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera." Ndondomeko ya muyaya: "Iyi ndi ya inu, ndi kwa ana anu; ichi chidzapatirira mpaka kudutsa mu m'badwo wa Mpingo uli wonse, kuchipereka icho kwa aliyense wa iwo."

125 O Mulungu, yeretsani manja anga. Yeretsani mtima wanga, Ambuye. Mulole, ngati ichi chichotsa bwenzi lililonse limene ine ndiri nalo, mulole ine ndipereke ndondomeko ya kamwedwe ka mankhwala iyi mu njira imene dokotala ananena kuti iyo iperekedwere.

Ichi ndi chifukwa chimene inu mukukhala ndi Mpingo yochulukwa yakufa, mamembala ochulukwa akufa. Inu mukuwonjezera zotetezera, ndipo mukuchotsa zochulukwa kuchokera ku iwo, mpakana ndondomeko kukhala yosathanthauza kwa iyo yokha. Iyo singachize kanthu kalikonse - kugwirana chanza, ku jowina Mpingo, ndi kukonkha. O, chifundo! Iyo sindondomeko ya kamwedwe ka mankhwala. Iyo ndi imfa.

Ngati inu mukufuna moyo, ndipo mukufuna Mzimu Woyera, tsatirani chimene Mulungu ananena kuti muchite. Tengani ndondomeko ya kamwedwe ka mankhwala. Iyo ndi ndendende njira imene iye ananena, "Inu musawonjezere ku iyo kapena kuchotsera ku iyo." Kenako akubwera pano chivumbulutso pamwamba pake ndi kunena kuti, "Ali yense amene adzachotsera kapena kuwonjezera ku ichi, ameneyo gawo lake

lidzachotseredwa mu buku la moyo." O, kalanga ine! Uyo ndi dokotala weniweni. O, Ine ndimamukonda Iye. Kodi inu simuli?

126 O, ku m'badwo waukulu, uwo m'badwo wa Aefeso, pamene mphekesera iyi basi inayamba ku kwawira mkati kupanga mabungwe, ndi azibusu ndi madikoni ... kapena osakhala madikoni, koma m'busu ... osati azibusu, koma makadinolo, mabishopu, mapapa, ma oyang'anira a Mpingo, kuwuwuza Mzimu Woyera, kuwuwuza Mpingo, "Tsopano inu simungakhale nacho chimenecho muno." Kodi bwana ndi ndani muli

monsemo?

Petula anafunsidwa chimenecho nthawi ina. Anati, "Inu simungalalikirenso mu Dzina la Yesu." Mutha kulalikira ngati mukufuna kutero, koma osati mu Dzina la Yesu." O, mdierekezi amadana nalo Dzina limenelo. Petro anati, "Kodi ichi ndi chabwino kwa ine kuti..." Baibulo linati, "Petro, pokhala wodzadza ndi chipembedzo" O, Mzimu Woyera. Anati, "Dikirani, mpakana ine ndipite ndikamuwone oyang'anira wamkulu, ndikawone chimene iye akandiwuze ine m'mene ndingachitire ndi ichi."

127 Ndiloleni ine ndikuuzeni inu. Kodi inu mukudziwa kuti a Assemblies of God ali ndi dokotala wa za ubongo wamisala kuti adziweruza, ndipo kupita kukawatenga a mishonare awo pamaso pa dokotala wa zaubongo kuti awone ngati munthu uyo ali bwino mu ubongo wake kuti angakhale wa mishonare? Pentekosite Assemblies of God. Ndiangati amene anayamba amvapo chimenecho? Ndithudi, ichi chiri ponseponse, aliyense. Ndithudi. Ndi ndani amene angamawayang'anire amishonare ndipo ndikukhala woweruza? Ndi dokotala wa zaubongo, kapena Mzimu Woyera? Mwaona, icho ndi chimene inu mumakhala nacho pokhala ndi munthu, mwaona, nthano zopangidwa ndi munthu, ziphunzitso zopangidwa ndi munthu. Dikirani mpakana ife titsikire ku m'badwo wa Pentekosite. Mulungu adzachiwotcha chinthu icho basi monga motsimikizira ngati dziko lapansi. Inde, bwana. Inde, ndithu. Ndipo inu mudzachiwona icho chikugwirira moto njira yonse pansu. Ndendende.

128 Koma tsiku lina la ulemerero Iye adzabwera.

Ndipo kumbukirani, mvetserani, pali mibadwo isanu ndi iwiri ya mipingo. Kodi uko nkulondola? Pali mibadwo isanu ndi iwiri ya Mpingo. Ndipo kumbukirani, pamene iwo anatuluka kukakumana ndi mkwati, ena anagona tulo, mu ulonda woyamba (kodi uko nkulondola?), muulonda wachiwiri (Osati kufa; kugona tulo), muulonda wachitatu, muulonda wachinayi, muulonda wachisanu, muulonda wachisanu ndi chimodzi. Ndipo muulonda wa chisanu ndi chiwiri liwu linabwera, "Tawonani mkwati akubwera! Tulukani inu kukakumana naye." Kodi chinachitika ndi chiyani? Anamwali onse aja amene anagona, anadzuka.

Mamawa uwo wowala ndi wopanda mitambo pamene

akufa mwa Khristu adzawuka (kopanda mitambo,

nyali zakumadzulo zidzawala),

Ndipo mamawa udzacha umuyaya, kowalala ndi kokongola;

Pamene opulumutsidwa pa dziko lapansi adzasonkhana

Kwao kuseri kwa mitambo,

Pamene azidzaitana mayina kumwamba uko ine ndidzakhala komweko.

Pamene azidzaitana mayina kumwamba uko,

Pamene azidzaitana mayina kumwamba uko,

Pamene azidzaitana mayina kumwamba uko,

Pamene azidzaitana mayina kumwamba uko, Ndidzakhala komweko.

Tiyeni timugwirire ntchito Ambuye kuchokera m'mawa mpakana kulowa kwa dzuwa,

Tiyeni tonse tiyankhule za chikondi chake chonse chodabwitsa ndi chisamaliro;

Ndiyeno pamene zonse zamoyo zidzatha, ndi ntchito yathu padziko lapansi idzatha,

Pamene azidzaitana mayina kumwamba,

Mwana aliyense wa Mulungu kwezani manja anu tsopano.

Pamene azidzaitana mayina kumwamba uko,

Pamene azidzaitana mayina kumwamba uko,

Pamene azidzaitana mayina kumwamba uko

Pamene azidzaitana mayina kumwamba uko,

Ndidzakhala komweko.

129 O, Mokoma patsogolo,

Ife tidzakumana pa Gombe lokongola apo;

Mokoma patsogolo,
 Ife tidzakumana pa Gombe lokongola apo.
 Kodi inu mumazikonda nyimbo zakale za mpingo?
 O, kwa Atate wathu wakumwamba wodzadza ndi zonse,
 Ife tidzapereka ulemu wathu wa matamando,
 ku mphatso ya ulemerero ya chikondi chake,
 Ndi madalaitso amene amakuta masiku athu.

Mokoma patsogolo
 Ife tidzakumana pa Gombe lokongola apo;
 Mokoma patsogolo
 Ife tidzakumana pa Gombe lokongola apo.

Tsopano gwiranani chanza ndi wina wake yemwe ali mokuzungulirani inu, pozungulira ngati chonchi. Izo ndi zabwino.

... mokoma patsogolo,
 (Nenani, "Ine ndidzakumana nanu, m'bale.")
 Ife tidzakumana pa Gombe lokongola apo;
 Mokoma patsogolo,
 Ife tidzakumana pa Gombe lokongola apo.
 Ife tidzayimba pagombe lokongolalo
 Nyimbo ya nthetemya
 (Aliyense ayiyimbe iyo tsopano.)
 Ndipo Mzimu wathu sudzamvaso chisoni,
 Osati mukuusa kwa madalitso athu a mpumulo.
 Aliyense, ndi manja ake okwezedwa m'mwamba;
 Mokoma patsogolo
 Ife tidzakumana pa Gombe lokongola apo;
 Mokoma patsogolo
 Ife tidzakumana pa Gombe lokongolalo.

130 Ndi mitu yathu yoweramitsidwa tsopano, tiyeni ife tiyankhule ichi [Anthu osonkhana akubwereza pa mbuyo pa m'bale Branham]: "Ambuye Yesu, ine ndimakundani Inu. Ine ndikukhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu, Mulungu kudzipanga kuwonetseredwa nthupi kuchotsa machimo anga. Ine sindikudalira kuthekera kwanga. Ine ndiribe. Koma ine modzipatula ndikudalira mu kuthekera kwa Yesu Khristu, amene ndi Mpulumutsi wa wanga, Mulungu wanga, Mfumu yanga. Ine ndimamukonda Iye. Ameni."

131 Mawa usiku 7 koloko, Ambuye akalola, ife tidzatenga Mpingo wa Smurna. Mokoma (ndi mitu yathu yoweramitsidwa tsopano)

patsogolo,
 Ife tidzakumana pa Gombe lokongola apo.
 (patsogolo);
 Mokoma patsogolo,
 Ife tidzakumana pa Gombe lokongolalo.
 Tsopano mofewa, aliyense, mokoma;

O, kwa Atate wathu wakumwamba mozadza ndi zonse,
Ife tidzapereka ulemu wathu wa wamatamando,
Kwa mphatso ya ulemerero ya chikondi chake.
Ndi madalitso amene amakuta masiku athu.
Mokoma patsogolo,
Ife tidzakumana pa Gombe lokongola apo;
Mokoma patsogolo,
Ife tidzakumana pa Gombe lokongolalo.



www.messagehub.info

Maulaliki wolalikidawa ndi
William Marrion Branham
"...mu masiku a liwu..." Chivumbulutso 10:7